bible educational services

# Buku la Mphunzitsi

## Nthawiyabaibulo
## Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi

Maphunziro B1 - B6

www.besweb.com

## Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

**Cholinga cha Utumiki**

Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

**Masomphenya a Utumiki**

Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

**Zomwe a Bible Educational Services amachita**

A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

**International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)**
Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA
Phone: 00 44 286 632 2462
Email: sam@besweb.com

**UK Secretary – Editorial feedback**
Mr Stephen Gillham
Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** www.besweb.com
**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: ***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

"Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa."

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

| | KALASI 0 (sanayambe sukulu)<br>Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7)<br>Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10) | Kalasi Yachitatu<br>(Zaka 11-13) | Kalasi Yachinayi<br>(Zaka 14+) |
|---|---|---|---|
| MAPHUNZIRO A | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Abrahamu<br>6. Abrahamu<br>7. Petro<br>8. Petro<br>9. Yakobo<br>10. Akhristu Oyambirira<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Pemphero<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe ndi Kugwa<br>2. Zochitika Zoyamba - Genesis<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Moyo wa Chikhristu<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO B | 1. Moyo Woyambirira wa Khristu<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Mafanizo<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Alembi a Uthenga Wabwino<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yakobo ndi Banja Lake<br>7. Yosefe<br>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Lamulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO C | 1. Danieli<br>2. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>3. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute ndi Samueli<br>6. Davide<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Yona<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>3. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Zoyankhula za Yesu<br>3. Mphamvu za Ambuye<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |

| | B1 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 1 – Mafanizo<br>Mutu – Kodi mnasi wanga ndi ndani? | B1 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 1 – Mafanizo<br>Mutu – Anthu angongole awiri |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 10: 25-37***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 10: 27***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Anansi athu ndi amene amafuna thandizo lathu ngakhale ndi a mtundu wina kapena chipembedzo china.<br>2. Ngati tikukonda Mulungu titha kuonetsa chikondi chathu pothandiza anansi pa moyo wawo wauzimu, wa kuthupi kapena pa zosowa zawo. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 7: 36-50***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aroma 5: 1***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Tonse tili ndi ngongole ya Ambuye Yesu Khristu - tonse tinachimwa choncho tili ndi ngongole ndi Mulungu.<br>2. Ngati anatikhululukira machimo athu, chikondi ndi kudzipereka kwa Ambuye Yesu Khristu ndiye zikhale chizindikiro cha miyoyo yathu mu chiyero ndi kutumikira. |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani tanthauzo la mnansi ndipo onetsani kuti si kukhala naye "pafupi" kumene kumapanga ife mnansi wabwino koma chifundo ndi ubale wathu zomwe timaonetsa kwa amene akusowa thandizo lathu posatengera kuti iwo ndi ndani. | Fotokozani zomwe zili m'fanizoli pofotokoza izi:<br>• Anthu atatu amene analipo – Ambuye Yesu, mayi wochimwa ndi Simoni Mfarisi.<br>• Anthu atatu oyerekeza – wokongoza, munthu anali ndi ngongole yokwana ndalama zasiliva 500, ndi munthu amene anali ndi ngongole yokwana ndalama zasiliva 50.<br>• Mafunso atatu – ***vesi 42, 44 ndi 49.*** |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. a) Munthu amene anavulazidwa ndi achifwamba, ***(vesi 30)*** anamuvula zovala, anamusiya ali pafupi kufa.<br>b) Wansembe ndi Mlevi anadutsa.<br>c) Msamariya anaonetsa chifundo ***(vesi 33)*** ndipo anamanga mabala ake ndi kupita naye ku nyumba ya alendo ndi kulamula kuti amusamalire mpaka iye atabweranso. ***(vesi 33-35)***<br>2. a) Chifukwa cha kusamvera kwa munthu m'Munda wa Edene, Mulungu amationa ngati akufa mu uchimo wathu. ***(Aefeso 2: 1)***<br>b) Mulungu anaonetsa chifundo chake kwa ife ochimwa ndipo anatumiza Mwana wake, Yesu Khristu, m'dziko lapansi kuti kudzera mu imfa yake ndi kuuka kwake tichiritsidwe ku tchimo lathu ndi ku zotsatira zake m'miyoyo yathu. Monga Msamariya Wachifundo, Yesu anabwera kumene kunali ife ndi kutithandiza.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kodi mnansi wanga ndi ndani? | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kudzilungamitsa kwa Simoni; misozi ya mayi yosonyeza kulapa, chimwemwe, chikondi ndi kuyamika; ndipo Ambuye Yesu anadziwa maganizo a Simoni akuti Yesu ankayenera kumuchotsa mayi wochimwayo. ***(vesi 36-39)***<br>2. Fanizo ili akufuna kuonetsa kuti Yesu ndi Wokongoza wathu. Ife tili ndi ngongole ndi Mulungu, ndipo pamene Yesu anafa pa mtanda, Iye anapereka ngongole yathu! Yesu anadziwa kuti Simoni ankadziona ngati wangongole ya masiliva 50 uja ndipo mayiyo ngati wamasiliva 500. Yesu ankafuna kuti Simoni aphunzire kuti palibe kusiyana pakati tchimo. Wa masiliva 50 ndi wa 500, onse ankalephera kubweza koma wokongoza uja anawakhululukira onse. ***(vesi 40-43)***<br>3. Pamene anafunsa kuti ndi wangongole uti amene akanakonda kwambiri wongongozayo, Simoni anavomereza kuti ndi amene anakhululukidwa zambiri. ***(vesi 42)*** Yesu anaonetsa Simoni 'mayi ameneyu' ndipo anafotokoza za chikondi chake pa Iye kusiyana ndi kupanda ulemu ndi chikondi kwa Simoni. ***(vesi 44)*** Yesu anafotokozanso kuti Iye amakhululukira machimo, koma chinali chikhulupiriro cha mayiyu, osati zomwe anachitazi, chinamupulumutsa. ***(vesi 48-50)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Anthu angongole awiri. |
| **KUKUMBUTSANA** | Funsani aliyense kuti mudziwe ngati amvetsa tanthauzo la fanizoli. Kukonda Mulungu ndi chinthu chabwino chomwe tingachite pa miyoyo yathu, ndipo timaonetsa kukonda Mulungu pamene tikondana wina ndi mnzake, posaona nkhope ya munthu amene akusowa chikondi. | Werengani ***Machitidwe 13: 38-39*** ndipo kambiranani mwachidule zomwe Yesu ankaphunzitsa m'phunziro limeneli. Werengani ***Aefeso 4: 32*** ndi kukambirana za khalidwe la amene akhululukidwa kwa ena ndi momwe akumvera mu mtima mwawo za kukhulukidwa kwawo ndi Mulungu machimo athu onse (kapena ngongole). |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi ophunzirawa anatembenuka mtima ndi kukhulupirira Yesu?<br>2. Ngati anatero, ganizani njira zomwe angaonetse kuti ndi anansi, kapena achikondi kwa anthu awa:<br>a) Munthu amene sanatembenuke mtima (mzimu)<br>b) Munthu wolumala (thupi)<br>c) Anthu amene alibe chakudya chokwanira madera ena pa dziko lapansi (zinthu) | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Simoni sanasamalire Ambuye Yesu moyenera ndipo palibe umboni woti analapa tchimo lake kuti akhululukidwe ndi kukhala ndi mtendere. ***(vesi 50)***<br>2. Kambiranani zomwe anachita kwa Ambuye Yesu, funsani ophunzira ngati analapa machimo awo ndi kubwera kwa Iye kuti awakhululukire?<br>3. Ngati anakhululukidwa, kodi amapereka kwa Ambuye Yesu nthawi yawo, maluso awo ndi zinthu zawo? Kambiranani zomwe anachita mayiyu. |

## B1 – KALASI Lachitatu
## Phunziro 2 – Mafanizo
## Mutu – Mlimi wachuma

**Ndime Yowerenga:** ***Luka 12: 13-21***
**Vesi Yoloweza:** ***Luka 12: 15***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Mlimi wachuma anali ndi zinthu zambiri koma anali wosauka moyo wauzimu, chifukwa m'moyo mwake munalibe Mulungu.
2. Ngati tiyika Mulungu kukhala woyamba, osati zinthu, Mulungu adzagwiritsa ntchito miyoyo yathu ku ulemerero wake, kaya tili ndi zambiri kapena zochepa.

### MAWU OYAMBA

Kambiranani zinthu zimene mumazikonda kwambiri.
Kambiranani za tchimo 'kusirira' ndi kutsimikizika kuti akumvetsa kuti kumeneku ndi kudzikonda kofuna kuti zonse pa dziko lapansi, zinthu zomwe siudzatenga ukadzamwalira. Onani Malamulo Khumi ndipo fotokozani kuti ndi chifukwa chiyani lamulo lomaliza likuti 'Usasirire'. ***(Eksodo 20: 17)***

### KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Yesu anamutcha munthu ameneyu 'wopusa' kusonyeza kusamvetsa kwake pa zinthu zofunika kwambiri zauzimu kuposa zinthu za dziko zimene ndi za kanthawi.
2. Iye anali 'wopusa' mu njira izi:
   a) Wopusa wopanda Mulungu – Iye ankakhala moyo wopanda Mulungu. Moyo wokhala ndi 'zinthu zambiri', koma osati ndi Mulungu, ndi moyo wopanda phindu. Iye sankadziwa kuti zinthu zake zonse zinkachokera kwa Mulungu.
   b) Wosauka wopusa – Iye anali wachuma wosauka – kusauka pa moyo wamuyaya. Iye ankadalira chuma m'malo modalira Mulungu.
   c) Wodzikonda wopusa – Pa ***vesi 17-19***, onani kasanu ndi kamodzi akuti **'Ine'**, kasanu akuti **'changa'**, ndipo kanayi akuti **'ndidza...'**. Mulungu, amene amapereka chuma, sanali m'maganizo mwake. Iye anatchula moyo wake kuti – moyo wanga!
   d) Wamatama wopusa – Iye anali wamatama chifukwa ankayankhula za moyo wake wabwino umene adzakhala kwa zaka zambiri, kupuma ndi kukwaniritsa zokhumba zake pakumadya ndi kumwerera. ***(vesi 19)***
   e) Wopusa watsoka – Mulungu amene anamuyiwala uja anati, "moyo wako udzachotsedwa." ***(vesi 20)*** Ndi Mulungu amene amapereka moyo ndipo angathe kuutenganso.

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro 2.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Mlimi wachuma.

### KUKUMBUTSANA

Mlimi wachuma anachita zolakwa zazikulu zitatu:
1. Iye sanamvetse tanthauzo la moyo. *Werengani **Afilipi 1: 21** ndi kufotokoza cholinga cha moyo wa Paulo.*
2. Iye anagwiritsa chuma cha ake pa iye yekha. *Werengani **Afilipi 4: 19** ndi kufotokoza momwe Mulungu amatisamalira pamene tikukwaniritsa zosowa za ena.*
3. Iye ankasamalira tsogolo lake ndi kutaya moyo wake. *Werengani **Marko 8: 36-37** ndi kukambirana momwe mavesi akukhudzira Mlimi Wachuma.*

### KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Lembani m'ndandanda wa zomwe tingachite pofuna kuthandiza ena ndi katundu wathu. Pezani kusiyana kwa 'zofuna ndi zosowa'.
2. Ganizirani za anthu amene si Akhristu kuti akuyenera kukhulupirira Yesu Khristu ***(Yohane 3: 16)*** kuti akhale woyamba m'miyoyo yawo.

## B1 – KALASI Lachinayi
## Phunziro 2 – Mafanizo
## Mutu – Kodi mnansi wanga ndi ndani?

**Ndime Yowerenga:** ***Luka 10: 25-37 ndi Afilipi 2: 1-11***
**Vesi Yoloweza:** ***Luka 10: 27***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Munthu amene akufunika kumuthandiza, posatengera mtundu wake kapena chipembedzo chake, ameneyo ndi mnansi ndipo ndi udindo wathu kumusamalira.
2. Kudzera mu imfa yake pa mtanda, Ambuye Yesu atha kutilanditsa, monga anachitira Msamariya uja. Iye atha kutiyika pa malo abwino ndi kutipatsa zosowa zathu. Onaninso Kalasi Lachitatu Phunziro Loyamba.

### MAWU OYAMBA

Kambiranani za kuti anansi athu ndi ndani.
Kambiranani ndi ophunzira kuti kukhala mnansi wabwino ndi khalidwe lokomera mtima ndi kuonetsa chikondi kwa osowa koma osati kukhala bwino ndi amene 'tayandikana nawo'. Yesu akuyembekezera kuti ana ake onse akhale wokoma mtima kwa aliyense kuphatikiza amene samatikonda – Moyo wapamwamba wa Chikhristu!

### KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Pamene katswiri wa Malamulo a Mose anafunsa Yesu zoyenera kuchita kuti akalandire moyo wosatha, Yesu anamuwuza za Malamulo ndi kumuwuza zomwe lamulo limafuna. Malamulo amafuna kukonda Mulungu kwathunthu ndi kukonda mnansi wako. Yesu akumuonetsa kuti cholinga cha Malamulo kapena Malamulo Khumi si kutipulumutsa ku tchimo koma kutionetsa kuti ndife ochimwa. ***(10: 26-28)***
2. Katswiri wa Malamulo ankayenera kumvetsa kulephera kwake kufika pa muyeso wa Mulungu ndi kupempha Ambuye kuti amupulumutse. Koma chifukwa cha kunyada kwake akufunsa Ambuye kuti, "Kodi mnansi wanga ndi ndani?" Pofuna kumuyankha, Ambuye akumuwuza nkhani ya Msamariya Wachifundo. Wansembe ndi Mlevi onse anali Ayuda amene ankadana ndi Asamariya. Iwo anakana kumuthandiza munthuyo koma Msamariya amene ankamunyoza ndi amene anabwera kudzathandiza wovulazidwayi. Mkulu wa malamulo anavomereza Msamariya ndiye anaonetsa kukhala mnansi weniweni kwa Myuda amene anavulazidwayo. ***(10: 29-37)***
3. Ife tikuona mwa Wansembe ndi mwa Mlevi kupanda mphamvu kwa Malamulo kuthandiza ochimwa ndipo Msamariya Wachifundo akutikumbutsa Ambuye Yesu amene anabwera kumene kunali ife, mu zosowa zathu, kudzatipulumutsa ku chilango chifukwa cha machimo.

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro 2.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kodi mnansi wanga ndi ndani?

### KUKUMBUTSANA

Onani Ndime Yowerenga m'buku la Afilipi ndipo tsirizani phunziroli mwachidule ***vesi 1-4*** pomwe akuyankhula za makhalidwe a mnansi mwa Akhristu ndi ***vesi 5-11*** pamene akuonetsa chitsanzo cha chikondi cha Ambuye Yesu pamene anafera anthu onse.

### KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
Munthu aliyense ndi mnansi:
1. Kodi tingathandize motani amene ali ndi zosowa za kuthupi, ku uzimu kapena zinthu zina?
2. Kodi pa ***Luka 6: 35*** akuti chiyani za anansi abwino? Kodi zimenezi tingazichite motani?

| | B1 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 3 – Mafanizo<br>Mutu – Wofesa mbewu | B1 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 3 – Mafanizo<br>Mutu – Munthu wopusa |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Marko 4: 1-20***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 4: 20***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mbewu ndi Mawu a Mulungu.<br>2. Mitundu yosiyana ya nthaka ikuyimira mitima ya anthu ndi zomwe amachita akamva Mawu a Mulungu | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 12: 13-21***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 12: 15***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kukhala wosirira ndi koyipa chifukwa munthu samakhala ndi katundu yekha.<br>2. Kukhala ndi mtima wodzikundikira chuma, mpaka kutaya moyo ndi kopusa kwambiri. Onani Kalasi Lachitatu Phunziro 2. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokoza kuti nthawi zambiri Yesu ankayankhula mafanizo pofuna kutsindika choonadi mu chiphunzitso chake. Nthawi zambiri mafanizo anali ndi tanthauzo lozama la uzimu. Nthawi zina sankafotokoza tanthauzo lake koma nthawi iyi anafotokoza tanthauzo lake. Malo osiyanasiyana amene mbewu inagwera inkayimira zomwe anthu amachita akamva Mawu a Mulungu. | Kambiranani zomwe zinachitika asanayankhule fanizoli. Munthu akupempha Yesu kuti aweruze mlandu wa kugawana katundu ndi m'bale wake. Kumbutsani ophunzira kuti Yesu akumuonetsa cholinga chomwe Iye anabwera kudzachita pa dziko lapansi chomwe ndi kupulumutsa anthu ochimwa osati kudzazenga milandu yogawana katundu. Izi ndi nkhani zochepa kuyerekeza ndi nkhani yofunika kwambiri ya moyo wauzimu yomwe ankayenera kuchitapo kanthu. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nthaka ya m'mbali mwa njira ***(vesi 15)*** ndi munthu amene amati "Amakana" Ambuye Yesu. Satana akufanizidwa ndi mbalame zomwe zimatenga Mawu. Munthuyo sakhulupirira Mawu a Mulungu.<br>2. Nthaka ya pa miyala ***(vesi 16-17)*** ndi munthu amene amamva Mawu ndi amaoneka ngati awalandira ndi kukhulupirira kwa kanthawi, koma mavuto akabwera ndipo akuyenera kukhala mbali ya Khristu, iye amaona kuti ndi zovuta kwambiri ndipo amasiya kutsatira Khristu. Mavuto akafika chikhulupiriro chomwe si chenicheni chimaonekera poyera.<br>3. Nthaka ya minga ***(vesi 18-19)*** ndi anthu amene amayamba bwino ndipo amaoneka ngati ndi Akhristu enieni. Koma, iwo amasangalatsidwa ndi ntchito zawo za malonda, chuma ndi zinthu zina za dziko lapansi kenaka amasiya kutchedwa Akhristu; iwo 'sabereka' zipatso.<br>4. Nthaka yabwino ***(vesi 20)*** ndi anthu amene amalandira Mawu – amatembenuka mtima ndi kusiya machimo awo ndi kukhulupirira Ambuye Yesu Khristu – ndi kumutsatira mokhulupirika mosatengera zomwe akumane nazo.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A –Wofesa mbewu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Fanizo ili likusonyeza kuti katundu si ndiye zofunika kwambiri m'moyo wathu. Mulungu ndiye amatipatsa ndipo tikuyenera kugwiritsa ntchito kuti Mulungu azilemekezeka. Munthu uyu ankayenera kuzindikira kuti ankayenera kupereka chuma chake chambiricho kwa osowa.<br>2. Iye anakonzekera za tsogolo – onani kuti akuchita yekha osati ndi Mulungu pamene akuti 'Ine' ndi 'changa' pa ***vesi 17-19***. Mulungu anali ndi chikonzero china ndipo anamuwuza kuti amwalira usiku umenewo ***(vesi 20)***. Chikonzero chake chikathera ku manda ndipo anali wopusa chifukwa sanakonzekere kumene akakhale moyo wake wamuyaya – onani chenjezo pa ***Amosi 4:12***.<br>3. Lozani pamene Mulungu akufunsa funso lofunika kwambiri mu fanizo limeneli, monga "Ndani amene adzatenga zimene iwe wadzikonzera?" ***(vesi 20)***<br>4. Fotokozani kuti tikuyenera kugwiritsa ntchito mphatso ndi maluso athu pofalitsa za ufumu wa Mulungu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Munthu wopusa. |
| **KUKUMBUTSANA** | Onetsetsani kuti ophunzira akumvetsa bwino za mitundu inayi yosiyana ya nthaka. Kambiranani za kusiyana kwa 'kubereka chipatso' pa ***vesi 20***; makumi atatu, makumi asanu ndi limodzi ndi zana limodzi ndipo onetsani kuti miyoyo yobereka zipatso kwambiri ndi anthu amene amadzipereka kumvera Mau a Mulungu ndi kuchita. | Onani zomwe zili pa ***Miyambo 11: 4 ndi 29*** ndi pa ***Mateyu 6: 19-21*** kuti ndi chidule cha phunziro lino. Onaninso pa ***Eksodo 20: 17*** pa nkhani ya kusirira. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi ndi nthaka iti imene ikufotokoza za mtima uliwonse?<br>2. Kwa Akhristu, kodi zotsatira za kukhala wa Ambuye Yesu pa sukulu kapena kulikonse ndi zotani?<br>3. Monga Mkhristu, ganizirani njira zina zomwe moyo utha kubereka zipatso pamaso pa Ambuye Yesu. Kodi ife tikufuna kubereka zotani – makumi atatu, makumi asanu ndi limodzi kapena zana limodzi?<br>4. Kuwerenga Baibulo, kuloweza vesi ndi kupemphera zimathandiza Mkhristu kukhala ndi mtima wabwino pamaso pa Mulungu ndi kubereka zipatsa m'miyoyo yawo. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kufunika kwa kudziwa cholinga cha moyo wake "Kwa ine kukhala ndi moyo ndi Khristu". (Paulo pa ***Afilipi 1: 21***)<br>2. Kufunika kogwiritsa ntchito chuma chathu kuthandiza anthu ena. Lembani maganizo anu a momwe mungathandizire anthu ena.<br>3. Kufunika kwa kusakhala ndi mtima wadyera ndi kusaganiza za chipulumutso. |

| | B1 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 4 – Mafanizo<br>Mutu – Kukhululukira ena | B1 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 4 – Mafanizo<br>Mutu – Phwando lalikulu |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 18: 21-35***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aefeso 4: 32***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Fanizo ili anaphunzitsa Akhristu za kukhululukirana.<br>2. Tikuyenera kukhululukira anthu ena mopanda malire. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 14: 15-24***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 6: 37***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu analonjeza phwando Kumwamba kwa onse amene anavomereza kuyitana kwake 'Bwerani kwa ine'. ***(Mateyu 11: 28)***<br>2. Kwa ife amene tinabwera kwa Ambuye Yesu ndi kupulumutsidwa tili ndi udindo olimbikitsa ena kuti alandire Yesu. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani vuto lomwe Petro anali nalo pa za kukhululukira. ***(18: 21)*** Fotokozani kuti iye ankadziwa kuti m'Chipangano Chakale munthu ankayenera kukhululukira mnzake katatu kapena kanayi ***(Amosi 2: 6)***. Monga wophunzira wa Ambuye Yesu, iye akuona kuti akuyenera kuonetsa mtima wachifundo pokhululukira kasanu ndi kawiri ***(vesi 21)***. Koma, Ambuye akuti, 'ka 70 kuchulukitsa ndi kasanu ndi kawiri' zomwe zikutanthauza kuti tikuyenera kukhululukira ena mopanda malire. | Fotokozani kuti mayiko a Kummawa, akuluakulu ankayitanidwa kawiri kuti apite ku phwando lomwe akonza. Kuyitana koyamba kunali kofotokozera anthu kuti akonza phwando ndipo kachiwiri kunali kuwauza kuti phwando lakonzedwa. Pa nkhani iyi amene anayitanidwa koma sankafuna kupita anayamba kupereka zifukwa zokanira. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Pamene mbuye wa antchito anazindikira kuti wangongole sakanatha kubweza, anamuchitira chifundo ndi kufuta ngongole yonse. ***(vesi 25-27)*** Ichi chinali chifundo, kusalanga munthu amene ankayenera kulangidwa.<br>2. Monga ochimwa, sitingathe kubweza ngongole yathu yayikulu ya tchimo ndipo tikufuna chifundo cha Mulungu kuti tipulumuke ku chilango chake. Ife timalandira chipulumutso chifukwa cha ntchito ya Khristu, amene analipira ngongole ya tchimo la dziko lapansi pa mtanda. Mulungu anapereka Mwana wake 'kukhala dipo la anthu ambiri'. ***(Mateyu 20: 28)***<br>3. Wantchito amene anakhululukidwa uja akanatha kukhululukiranso mnzake amene anamukongola zochepa (pafupifupi 5,000 kwacha) kusiyana ndi zomwe iye anakongola zomwe zinali (pafupifupi 1 biliyoni kwacha). Iye anayiwala chifundo chomwe anamuonetsa.<br>4. Ife tikuyenera kuchitira anzathu zomwe Ambuye Yesu anatichitira. Ngati timanena kuti ndife ake, tikuyenera kukhululukira ena, kuphatikiza adani athu. ***(Onani Vesi Yoloweza.)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhululukira ena. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. 'Phwando Lalikulu' limeneli likutikumbutsa kuti Ambuye Yesu anatsiriza ntchito yawo ya chipulumutso potifera pa mtanda ndipo zotsatira zake ndi Uthenga Wabwino umene ukuyitana aliyense.<br>2. Zifukwa za anthu atatu amenewa sizinali zoona chifukwa iwo akanatha kuchita zinthu zomwe zikanawalola kuti akhale nawo pa phwando limeneli: Chifukwa choyamba ***(vesi 18)***: kulephera chifukwa anagula munda. N'kovuta kukhulupirira kuti Myuda akanagula munda asanawuone komanso podziwa kuti phwando linali la usiku sakanatha kupita kukaona munda nthawi imeneyi. Chifukwa chachiwiri ***(vesi 19)***: Munthu uyu ndi wachipongwe, sakupepesa za kulephera kwake ndipo kwa iye akuona kuti ng'ombe zake ndi zofunika kwambiri. Chifukwa chachitatu ***(vesi 20)***: Munthu uyu akupereka chifukwa chosamveka popeza akanatha kupita ku phwando ndi mkazi wakeyo akanakhala kuti si wodzikonda.<br>3. Chifukwa choyamba chikuyimira anthu amene amayika mtima wawo kwambiri pa chuma chawo, chifukwa chachiwiri ndi anthu amene ndi otanganidwa kwambiri ndi ntchito zawo, ndipo chachitatu ndi anthu amene amatanganidwa kwambiri ndi ntchito za pa khomo pawo.<br>4. Mwini phwando wayipidwa kwambiri ndipo akuona kuti amuchita chipongwe popereka zifukwa zimenezi ndipo akutumiza antchito ake 'kupita kunja m'misewu ndi m'makwalala' kukayitana osauka, olumala ndi osaona. ***(vesi 21 ndi 23)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Phwando lalikulu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Kambiranani momwe ndime imeneyi ikuonetsera za 'chifundo' ndi 'chisomo'. Phunzirani ***Tito 3: 5***. "Zosati zochokera m'ntchito za m'chilungamo, zimene tidazichita ife, komatu monga mwa chifundo chake anatipulumutsa ife…" Fotokozani kuti chifundo chimabweretsa chilungamo cha Mulungu kuti tipulumuke ku chilango chake. Phunzirani ***Aefeso 2: 8***. "Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo." Kupulumutsidwa ndi mphatso ya Mulungu yomwe imabwera mwachisomo – kutipatsa chitetezo chamuyaya chimene ndi chosatiyenera, sitigwira ntchito kuti tichepeze. | Fotokozani kuti fanizo limeneli likuonetsa kuti Uthenga Wabwino unayamba kuperekedwa kwa Ayuda, ndipo, ataukana, anaupereka kwa anthu Amitundu ina amene anaulandira mwachidwi. Onetsetsani kuti ophunzira amvetsa za kufunika kwake kwa iwo amene akupitiriza kukana chifundo ndi chisomo cha Ambuye chifukwa tsiku lina nthawi idzakhala itatha, ndipo makomo a Uthenga Wabwino wa phwando la Kumwamba adzakhala atatsekeka.<br>Ganizani zifukwa zina zomwe anthu akupereka lero popakana Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi tikuphunzira chiyani za 'kukhululukira'?<br>2. Ngati tinakhululukidwa ndi Ambuye Yesu, n'chifukwa chiyani tikuyenera kukhululukira ena?<br>3. Onani ***Aefeso 4: 32*** kuti mupeze makhalidwe ena amene tiyenera kukhala nawo kuonjezera pa 'kukhululukira'. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Palibe munthu amene ndi woyipa kwambiri kuti sangathe kukhala pa chakudya chachifumu monga taona za anthu amene anachokera 'm'misewu ndi m'makwalala.'<br>2. Tikuyenera kukopa ena mwachikondi kuti alandire madalitso a chipulumutso. Muli malo ambiri mu ufumu wa Mulungu oti anthu alowemo. |

| | B2 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 1 – Zodabwitsa<br>Mutu – Madzi asanduka vinyo | B2 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 1 – Zodabwitsa<br>Mutu – Madzi asanduka vinyo |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 2: 1-11***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 2: 11***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Tikuyenera kumvera Ambuye Yesu.<br>2. Pamene takhulupirira Ambuye Yesu, Iye amabweretsa chimwemwe m'mitima mwathu. | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 2: 1-11***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 2: 5, Yohane 15: 14***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ngati timakonda Ambuye Yesu, tikuyenera kumvera malangizo a Mariya kwa antchito aja pa ukwati: "Inu muchite chilichonse chimene akuwuzeni." ***(Yohane 2: 5)***<br>2. Pochita chodabwitsa ichi, Ambuye Yesu anaonetsa kwa onse amene anali pamenepo kuti Iye ndi Mulungu m'thupi la munthu, potero analimbikitsa chikhulupiriro cha ophunzira ake aja. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani machitidwe a maukwati a ku Mayiko a Kummawa. Fotokozani kuti mu ndime iyi Mariya akutchedwa 'amayi a Yesu' pa ***vesi 1***. Fotokozani kuti Ambuye Yesu sanatchuke chifukwa anali mwana wa Mariya Virigo koma Mariya ndiye anatchuka kwambiri chifukwa anali mayi wa Ambuye. Tsindikani kuti Baibulo limapereka ulemu waukulu kwa Ambuye Yesu osati kwa Mariya. | Kambiranani tanthauzo la zodabwitsa ndi chifukwa chomwe analemba mu Uthenga Wabwino.<br>Uthenga Wabwino wa Yohane wamangika pa zodabwitsa zisanu ndi ziwiri, zonse anazichita pagulu ndipo choyamba ndi cha ku ukwati wa ku Kana ku Galileya. Ophunzira afunsidwe kupeza pamene pali zodabwitsa zina.<br>Fotokozaninso za machitidwe a ukwati wa ku Mayiko a Kummawa. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Chisankho choyitana Ambuye Yesu ku ukwati chinali chanzeru kwambiri monganso kumuyitana Iye kuti alowe m'mitima mwathu, m'nyumba mwathu, pa zochita zathu ndi pa maphunziro athu.<br>2. Alendo anakhumudwa pamene vinyo anatha phwando la ukwati litayamba kumene, koma izi zitachitika, iwo anapita kwa Ambuye Yesu kupempha thandizo. ***(2: 4 ndi 5)***<br>3. Vinyo wabwino anabwera kumapeto kuti atikumbutse ife kuti moyo wa Chikhristu ndi wabwino nthawi zonse.<br>4. Chodabwitsa ichi chinaonetsa kuti Khristu ndi Mwana wa Mulungu ndi kulimbikitsa chikhulupiriro cha ophunzira ake. ***(2: 11)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Madzi asanduka vinyo. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ambuye Yesu, amayi awo ndi ophunzira anali alendo pa ukwati kumene madzi anasanduka vinyo.<br>2. Mariya analozera antchito kwa Ambuye Yesu ndipo m'mawu ake otsiriza kulembedwa anakuwuza antchito kuti: "Inu muchite chilichonse chimene akuwuzeni" kulozera amene anali pamenepo kwa Ambuye Yesu osati kwa munthu wina aliyense. ***(2: 4 ndi 5)***<br>3. Vinyo wabwino anaperekedwa kumapeto kwa ukwati umenewu, koma mmene ankachitira nthawi imeneyi ankayenera kupereka vinyo wabwino poyamba.<br>4. Chodabwitsa ichi chinaonetsa kuti Khristu ndi Mwana wa Mulungu ndipo chinalimbikitsa chikhulupiriro cha ophunzira ake. ***(2: 11)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Madzi asanduka vinyo. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani kuona chodabwitsa ichi kudzera m'mafunso amene amathandiza ana kuyankha mafunso a mu KALASI Lachitatu, B2, Phunziro 1. | Bwerezani phunziroli pogwiritsa ntchito fundo iliyonse pa moyo wa Chikhristu. Dziwani:<br>1. Vinyo m'Baibulo amatanthauza chimwemwe. Pamene Mariya anati: "Wawathera vinyo" ***(vesi 3)***, iye ankafotokoza za amene sanakhulupirire Ambuye Yesu chifukwa osakhulupirira alibe chimwemwe chokhalitsa.<br>2. Iwo amene amakonda Ambuye Yesu amachita zimene Iye amanena m'Mawu ake – Baibulo.<br>3. Yesu akuonekera poyera kuti ndi Mwana wa Mulungu. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kambiranani tanthauzo la kuyitana Ambuye Yesu m'mtima yanu. Werengani ***Miyambo 3: 5-6*** kuti mudziwe momwe Ambuye adzakuthandizireni kukhala moyo wopindulitsa kwa Iye.<br>2. Werengani ***Salimo 16: 11*** kuti muone chimwemwe chimene chikudikira amene amadziwa Ambuye Yesu ngati Mpulumutsi wawo pamene akafika Kumwamba. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ganizirani momwe timakhulupirira Ambuye Yesu monga Mpulumutsi wathu.<br>2. Kambiranani kufunika kowerenga Baibulo ndi kupemphera nthawi zonse kuti tidziwe chifuniro cha Ambuye pa miyoyo yathu. |

| | B2 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 2 – Zodabwitsa<br>Mutu – Kuchiritsidwa kwa mwana | B2 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 2 – Zodabwitsa<br>Mutu – Mwana achiritsidwa |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 4: 43-54***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 4: 50***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mwana wa nduna ina ankadwala kwambiri ndipo anali pafupi kumwalira. Iye anali kutali ndi kumene kunali Yesu koma anachiritsidwa ndi Yesu.<br>2. Tonse tinabadwa ochimwa komanso kutali ndi Ambuye Yesu koma pamene tatembenuka mtima ndi kubwera kwa Iye kuti atikhululukire, Iye amatipatsa moyo watsopano. | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 4: 43-54***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 16: 31, Aroma 10: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mwana wa nduna imeneyi anali pafupi kufa, koma ndi Ambuye Yesu wokha amene anali ndi mphamvu zomuchiritsa kuti akhale ndi moyo.<br>2. Tchimo lathu ndi matenda, matenda auzimu, amene adzabweretsa imfa yauzimu ndipo ndi Ambuye Yesu wokha amene angatipatse ife moyo wosatha. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ophunzira kuti Ambuye Yesu, pa ulendo wake woyamba ku Kana, anasandutsa madzi kukhala vinyo ndipo apa anthu anali pafupi kuonanso chodabwitsa china champhamvu ku Kana komweko –kuchiritsidwa kwa mwana wa nduna.<br>Gwiritsani ntchito mapu a m'phunziroli kuti muone kuti Yesu anali ku Kana ndipo mnyamatayu anali ku Kapernao pamene mphamvu za Yesu zinamukhudza kumeneko ngakhale sanali kumene kunali Yesu. | Kumbutsani ophunzira kuti Ambuye Yesu anachita chodabwitsa ichi ku Kana komwe anachita chodabwitsa chake choyamba chija ndipo mbiri yake inafalikira konse, kotero kuti abambo a mnyamatayu, nduna ya Herode, modzichepetsa anapempha kuti achiritse mwana wake.<br>Ndunayi inkaganiza kuti Ambuye Yesu ankayenera kupita kukachiritsa mwana wake. Ambuye Yesu sanamudzudzule chifukwa chopanda chikhulupiriro kwake koma anamupatsa mphotho chifukwa cha chikhulupiriro chomwe anaonetsa ndi kumupatsa zambiri. Fotokozani kuti Ambuye Yesu sanakondwere ndi chikhulupiriro choti mwana wake atha kuchiritsidwa koma ndi chikhulupiriro cha pa mawu ake – yambani kukhulupirira kenaka ndi kuona! |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Bambo a mnayamatayu anali Myuda ndiponso nduna ya Mfumu Herode. Iye anali ndi chikhulupiriro chachikulu pa Ambuye Yesu kusiyana ndi Ayuda ena onse ndipo anapempha Ambuye kuti achiritse mwana wake chifukwa ankadwala kwambiri. ***(4: 47)***<br>2. Abambo a mnyamatayu ankaganiza kuti Ambuye Yesu ankayenera kupita kumene kunali mwanayo, koma Ambuye anamuwuza kuti mwana wake achiritsidwa ndipo ndunayi inakhulupirira mawu a Ambuye ndi kunyamuka kubwerera kwawo. ***(4: 50)***<br>3. Pamene anafunsa antchito ake nthawi imene mnyamatayo anachira, yankho lawo limaonetsa kuti inali nthawi yomwe Ambuye Yesu anamuwuza kuti mwana wake wachira. ***(4: 52-53)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 2.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuchiritsidwa kwa mwana. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. **Za mnyamata odwala ndi pempho la abambo ake.** Matenda ndi imfa zimabwera kwa munthu aliyense, achuma kapena osauka, koma aliyense akufunika Ambuye Yesu kuti akwaniritse zosowa zawo zauzimu. Ambuye Yesu amatenga kuti tchimo ndi matenda – onani pa ***Mateyu 9: 12-13***. Baibulo limaphunzitsa kuti amene amadziwa Ambuye Yesu ali ndi moyo wosatha ndipo amene sadziwa Iye alibe moyo wosatha. ***(1 Yohane 5: 10-14)***<br>2. **Yankho la Ambuye.** Ambuye Yesu ankayesa chikhulupiriro cha nduna imeneyi pamene anayiwuza kuti 'mwana wako adzakhala ndi moyo' ***(vesi 50)***. Anthu a masikuwa, monga leronso, ankafuna kuona zizindikiro ndi zodabwitsa ***(vesi 48)*** m'malo movomereza Mawu a Mulungu chomwe akunena: chikhulupiriro poyamba, kenaka kuona!<br>3. **Zotsatira.** Mawu a Mulungu ndi amoyo ndipo kudzera mwa iwo titha kudziwa Ambuye Yesu monga Mpulumutsi wathu komanso ndi kulimbikitsidwa, chifukwa Mawuwa ndi mphamvu ya Mulungu. Ndunayi inakhulupirira, mwana wake anachiritsidwa, ndipo banja lake lonse linakhulupirira.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 2.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Mwana achiritsidwa. |
| **KUKUMBUTSANA** | Phunzirani Vesi Yoloweza, ***Yohane 4: 50***. Kambiranani zomwe ikufotoza za phunziro lino kuti mphamvu ya Ambuye Yesu Khristu sinangochiritsa mnyamata yekhayu komanso banja lonse la ndunayi linakhulupirira Yesu ***(Yohane 4:53)***. | Ganizirani mawu ochokera pa ***Ahebri 11: 6***: 'Popanda chikhulupiriro n'kosatheka kukondweretsa Mulungu', ndipo kambiranani kuti zikukhudza motani ophunzira kuchokera pa zimene aphunzira. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Tonse tikuyenera kukhulupirira ndi kumvera Ambuye Yesu ndi mitima yathu yonse kuti tikhale ndi moyo wosatha.<br>2. Monga Akhristu aang'ono, tikuyenera kuyamika kuti Ambuye Yesu sakuyenera kukhala nafe m'thupi kuti achite chodabwitsa kapena kuyankha pemphero lathu chifukwa Iye atha kukwaniritsa chifuniro chake kuchokera kulikonse kumene ali nthawi ina iliyonse. Izi zitilimbikitse pa moyo wathu wapemphero. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ndunayi inakhulupirira Ambuye Yesu ndipo inanyamuka kupita kwawo – iyo inaonetsa chikhulupiriro chake. Ganizirani njira zomwe tingaonetsere chikhulupiriro chathu pa nyumba kapena ku sukulu.<br>2. Kodi kukhulupirira Ambuye Yesu ndi kovuta motani kumene tikukhalako lero? (Nenani za anthu amene akufuna kuyamba kuona kenaka ndi kukhulupirira, mosiyana ndi amene amakhulupirira kenaka ndi kuona chifuniro cha Ambuye pa miyoyo yawo kuchokera m'Mawu ake.) |

| | **B2 – KALASI Lachitatu**<br>**Phunziro 3 – Zodabwitsa**<br>**Mutu – Kutsekula maso osaona** | **B2 – KALASI Lachinayi**<br>**Phunziro 3 – Zodabwitsa**<br>**Mutu – Bartimeyu wosaona** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Marko 10: 46-52***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 10: 52***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Bartimeyu anali ndi chosowa chachikulu, iye ankadziwa chosowa chake ndipo anatsimikiza mtima kuti Ambuye Yesu akwaniritsa chosowa chakecho.<br>2. Ambuye Yesu anayankha pemphero la Bartimeyu ndipo iye anaonetsa kuyamika kwake pa kutsatira Ambuye Yesu pa ulendo wake wopita ku Yerusalemu. | **Ndime Yowerenga:** ***Marko 10: 46-52***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 10: 52***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Monga mmene anayitanira Bartimeyu ***(vesi 49)*** moteronso Ambuye Yesu akuyitani amene ndi wosaona mu uzimu, kudzera mu kulalikira kwa Uthenga Wabwino.<br>2. Pamene takhulupirira Ambuye Yesu kuti atipulumutse, tikuyenera kusiya moyo wathu wauchimo ndi kumutsatira. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ophunzira ngati akudziwa munthu wina amene ndi wosaona ndipo afotokoze mavuto amene amakumana nawo pa moyo wake. Kambiranani momwe anthu angathandizire anthu osaona amene sangathe kuchiritsidwa. | Fotokozani kuti nthawi imeneyo wosaona ankalandira thandizo lochepa komanso losakwanira; anthu osaona ambiri a nthawi ya Ambuye Yesu ankapeza thandizo lawo pomapempha. Siyanitsani ndi zomwe zimachitika lero. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Bartimeyu wosaona anali Myuda, ndipo iye anakhulupirira kuti Yesu anali Mesiya, Mwana wa Davide. Ayuda ambiri sankakhulupirira kuti Yesu anali Mesiya. ***(11: 47)***<br>2. Bartimeyu anapitiriza kupempha thandizo kwa Yesu kuti amuchiritse ngakhale ena ankamuwuza kuti akhale chete. Ambuye Yesu, Mlengi wa Kumwamba ndi dziko lapansi ndi mwini dziko lonse, 'anayima' ***(11: 49)*** atamva kufuula kwa munthu wopempha uja ndi kubwezeretsa kuona kwake!<br>3. Bartimeyu anaonetsa kuyamika kwake pokhala wotsatira wa Yesu wokhulupirika, paulendo womaliza wopita ku Yerusalemu asanapachikidwe pa mtanda. ***(11: 52)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kutsekula maso osaona. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Bartimeyu anali wosaona ndiponso wosauka, kutikumbutsa ife kuti ndife osaona ku zauzimu ndipo chifukwa cha chimenecho sitikudziwa kumene tikupita.<br>2. Uwu mwina unali mwayi womaliza wa Bartimeyu kuti akumane ndi Ambuye Yesu, motero anapempha Ambuye Yesu kuchokera pansi pa mtima: 'mundichitire chifundo ine' ***(vesi 47)***. Chipulumutso ndi cha munthu pa yekha n'chifukwa chake iye akuti 'ine'.<br>3. Bartimeyu anataya zonse zimene zikanamulepheretsa kupita kwa Ambuye Yesu ndipo atapempha zoti aonenso anapatsidwa nthawi yomweyo. Ili nkhani monga 'chikondi m'maso' pakuti anayamba kutsatira Ambuye Yesu nthawi yomweyo. ***(vesi 50-52)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Bartimeyu wosaona. |
| **KUKUMBUTSANA** | Onetseni pemphero lalifupi la Bartimeyu pa ***vesi 51*** ndi yankho la Yesu pa ***vesi 52***. Monga Yesu anafunsa Bartimeyu chimene ankafuna kuti amuchitire, titha kuphunzira kufunika kodalira Ambuye Yesu msanga chifukwa mpata wotere supezeka kawirikawiri kwa ife. Ngati Bartimeyu akanataya mwayi umenewu, mwina sakanathanso kukumana ndi Ambuye Yesu. (Onani ***Yohane 8: 12***) | Onani pa ***Mateyu 4: 18-22*** ndipo pezani ena amene anasiya nthawi yomweyo zomwe ankachita ndi kutsatira Ambuye Yesu.<br>Onani pa ***Aefeso 6: 10-18*** ndi/kapena ***Akolose 3: 8-17*** kuti mupeze makhalidwe amene Ambuye Yesu amawafuna kwa amene akumutsatira.<br>Kuchokera pa zomwe tawerenga m'Baibulo, lembani fundo zazikulu zisanu ndi chimodzi zomwe zikuyenera kukhala m'moyo wa Mkhristu. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Chinali chosangalatsa kwa Ambuye Yesu kuona Myuda wosaona wayamba kuona mwa uzimu ndipo akumutsatira. Aliyense akuyenera kukhulupirira Ambuye Yesu ndi kumukondweretsa pomutsatira Iye.<br>2. Mapemphero athu sakuyenera kukhala aatali. Ife titha kuwuza Ambuye Yesu kuti timawakonda ndi kufunsa chomwe akufuna kuti ife tichite.<br>3. Funsani aliyense apemphere pemphero lalifupi, lofunika molingana ndi zosowa zawo. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kufunika kwa kufuna Ambuye Yesu kuti atipulumutse, pamene Iye akuyitana komanso nthawi ikanalipo.<br>2. Pamene tili otsatira a Ambuye Yesu, mphamvu yake imagwira ntchito m'miyoyo yathu ndipo titha kugwiritsidwa ntchito yomukondweretsa pochita chifuniro chake. Ife tasiya moyo wathu wakale wauchimo ndipo tayamba moyo watsopano ndi Ambuye Yesu.<br>3. Werengani ***Yohane 8: 12*** ndipo ganizirani tanthauzo la kusiya ntchito za mdima ndi kuyamba "Kuyenda mu kuunika". |

| | B2 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 4 – Zodabwitsa<br>Mutu – Kuchiritsidwa kwa anthu khumi akhate | B2 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 4 – Zodabwitsa<br>Mutu – Amuna khumi akhate |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 17: 11-19***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Salimo 107: 8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ndi Ambuye Yesu wokha amene angatiyeretse ife ku machimo athu.<br>2. Amene ayeretsedwa akuyenera kuonetsa kuyamika kwawo pakutumikira Ambuye Yesu mwachikondi ndi modzipereka. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 17: 11-19***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aefeso 2: 8-9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ife tinabadwa ochimwa ndipo nthenda ya tchimo amene angathe kuchiritsa ndi Ambuye Yesu.<br>2. Pamene tachira ku nthenda ya uchimo tikakhulupirira Ambuye Yesu, tikuyenera kumathokoza nthawi zonse chifukwa cha dalitso la chipulumutso ndi zinthu zina zonse zabwino zimene timalandira kuchokera kwa Iye tsiku lililonse. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani kuti khate ndi nthenda ya pa khungu imene imagwira anthu ambiri pa dziko lapansi.<br>Onani pa ***Levitiko 13: 45-46*** ndipo fotokozani kuti akhate ankatengedwa kukhala anthu odetsedwa mu nthawi ya Mose komanso ankakhala kwa okha. Izi zinalinso chomwecho mu nthawi ya Yesu. | Fotokozani kuti khate ndi matenda opatsirana a pa khungu amene alipo lero pa dziko lapansi. Amati mwina pa dziko lapansi pali anthu 20 miliyoni amene ali ndi matendawa. Mwina ena munamvapo za ‘Utumiki kwa Akhate’– ili bungwe limene limathandiza anthu amene akudwala matenda amenewa.<br>Onani anthu ena m’Baibulo amene anadwala matenda a khate. Onaninso pa ***Levitiko 13: 45-46***. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Akhate sankaloledwa kukhala pakati pa anthu ena, n’chifukwa chake iwo anafuula kwa Ambuye Yesu kuti awachitire chifundo ali kutali. ***(17: 12-13)***<br>2. Pomvera Ambuye Yesu, akhate ananyamuka ulendo wopita ku nyumba ya wansembe, ndipo atafika ku nyumbayo anaona kuti anali atachira khate lija. ***(17: 14)***<br>3. Ndi wansembe amene anawapatsa chilolezo kuti apite ku mabanja awo.<br>4. Wakhate mmodzi yekha, Msamariya, anabwerera kudzathokoza Ambuye Yesu chifukwa chomuchiritsa. ***(17: 15-19)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuchiritsidwa kwa anthu khumi akhate. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Akhate sakanatha kudzichiritsa okha koma anabwera kwa munthu woyenera, Ambuye Yesu, kuti awachitire chifundo. ***(vesi 13)***<br>2. Pamene Ambuye anati ‘Pitani’ ***(vesi 14)***, akhate anamvera mawu ake ndipo anayeretsedwa ali m’njira akupita ku nyumba ya wansembe. Kumvera ndi kukhulupirira Mawu a Ambuye kunawayeretsa.<br>3. Wakhate mmodzi yekha, Msamariya, ndiye anabwerera modzichepetsa kudzathokoza ndi kupembedza ***(vesi 16)*** Ambuye Yesu chifukwa cha mphatso ya kuyeretsedwa.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze**.<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Amuna khumi akhate. |
| **KUKUMBUTSANA** | • Onaninso phunziroli pofotokoza momwe khate likufananira ndi munthu wochimwa amene ali kutali ndi Ambuye Yesu. Kumbutsani aliyense kuti machimo ake atha kuyeretsedwa pamene apempha Ambuye Yesu kuti amukhululukire ndi kumvera Uthenga Wabwino. Uthenga Wabwino umafotokoza za imfa ya Khristu ndi kuuka kwake kwa akufa.<br>• Phunziro likuphunzitsa kuti pamene tayeretsedwa tchimo lathu, tikuyenera kumathokoza Ambuye Yesu nthawi zonse chifukwa cha chipulumutso chathu. Kuthokoza ndi chizindikiro cha amene amakonda Ambuye Yesu. | Funsani ophunzira pa phunziro limeneli monga njira yobwereza zomwe aphunzira komanso kukonzekera kuyankha mafunso Nthawiyabaibulo. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Ganizira ***1 Yohane 1: 9*** ndi za kufunika kwake.<br>2. Akhristu akuyenera kuthokoza Ambuye Yesu chifukwa chowafera.<br>3. Ntchito ya gulu – lembani zinthu zimene ife tikuyenera kukhala othokoza ndi kulemba pemphero lake. | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Onani ngati ophunzira anu ali ngati mmodzi mwa akhate asanu ndi anayi kapena ngati wakhate mmodzi uja.<br>2. Kambiranani tanthauza la kuthokoza ndi momwe zikukhudzira miyoyo yathu - ***Salimo 40: 3***.<br>3. Ntchito ya gulu – lembani zinthu zimene ife tikuyenera kukhala othokoza ndi kulemba pemphero lake. |

| | B3 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 1 – Betaniya<br>Mutu – Alongo awiri | B3 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 1 – Betaniya<br>Mutu – M'nyumba |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 10: 38-42***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 10: 42***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ambuye Yesu amakondwera ndi chikondi chathu pa Iye kuposa kutumikira kwathu.<br>2. Ntchito za m'nyumba mwathu, kapena ku sukulu tisalole kuti zitchinge moyo wapemphero ndi nthawi yowerenga Mawu a Mulungu. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 10: 38-42***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 6: 31***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kuti tikule pa moyo wathu wa Chikhristu, tikuyenera kukhala ndi nthawi m'kati mwa kutanganidwa kwathu yowerenga Mawu a Mulungu ndi cholinga choti timve zimene Mulungu akuyankhula kwa ife.<br>2. Tikuyenera kukhala ndi nthawi m'kati mwa kutanganidwa kwathu yopemphera kuti tiziyankhula ndi Mulungu ndi kumuthokoza chifukwa cha ubwino wake wonse komanso kupempha kuti atitsogolere m'miyoyo yathu. |
| MAWU OYAMBA | Funsani ophunzira kuti aganizire momwe akanamva mu mtima mwawo ngati m'nyumba mwawo mukanabwera munthu wofunika kwambiri. Nyumba ya Mariya ndi Marita inali imodzi mwa nyumba zimene Yesu ankapitako. Aliyense aganize nyumba zina kumene Yesu ankapitako: ***Luka 4: 38, Luka 7: 37, Luka 8: 51, Luka 19: 5.***<br>M'nyumba zathu zikhale malo amene Ambuye Yesu amalandira ulemu ndi kumumvera. | Fotokozani kuti Mariya ndi Marita onse awiri ankakonda Yesu. Pa nthawi imeneyi onse ankamutumikira Iye. Marita sankazindikira kuti kukhala otanganidwa ankalephera kukwaniritsa zolinga za mlendo wake – Ambuye Yesu – iye analibe nthawi yomvera ndi kuphunzira kuchokera kwa Iye. Funsani ophunzira anu zomwe ndi zofunika kuchita m'miyoyo yawo. Yesetsani ndi kuonetsetsa kuti akumvetsetsa 'kutanganidwa' si koyenera kulowa m'malo mwa pemphero ndi kuphunzira Baibulo. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Pamene Marita anali 'wantchito', Mariya anali 'wopembedza'. Ntchito ndi kupembedza zikuyenera kuyendera limodzi. *Kambiranani tanthauzo la kupembedza.*<br>2. Ngakhale Marita ankafuna kupereka ulemu kwa Ambuye Yesu kudzera mu kumuphikira chakudya chokoma, Iye ankakondwera ndi chiyanjano chawo. N'chifukwa anayankhula za Mariya kuti, 'wasankha chinthu chabwino' ***(vesi 42)***. Chakudya cha moyo wathu wauzimu ndi chofunika kwambiri kuposa chakudya cha thupi ndipo Ambuye Yesu ankafuna onse Mariya ndi Marita kuti amvetsetse kufunika kwa kumva Mawu ake. ***(1 Petro 2: 2)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Alongo awiri. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ambuye anakhazikitsa chidwi chawo pa Pemphero ndi Kuphunzira Baibulo zomwe ndi zinthu ziwiri zofunika kuti tidalitsike pa miyoyo yathu.<br>2. Yesu sanaloze chala Marita chifukwa chotanganidwa ndi ntchito ya pa khomo koma anamulangiza mofatsa chifukwa cha masinkhidwe ake pa zochita zake.<br>3. Ambuye Yesu akuyankhula pa ***vesi 42*** kuti kuyika chidwi pa Iye ndiye chinthu chofunika kwambiri. Iye amalemekeza kwambiri chikondi chathu kuposa kutumikira kwathu. Ambuye akufuna kuti tisinthe kuchoka pokhala 'Marita' ndi kukhala 'Mariya.'<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – M'nyumba. |
| KUKUMBUTSANA | N'zopatsa chidwi kuona kuti Mariya 'anakhala pa mapazi a Yesu' ***(vesi 39)***. Kambiranani zomwe Mariya anachita pokhala pamalo onyozeka ngati amenewa zomwe zinkatanthauza kulemekeza ndi kupereka ulemu woyenera kwa Ambuye Yesu.<br>1. Funsani zomwe ife tingachite pofuna kulemekeza ndi kupereka ulemu kwa Ambuye Yesu m'miyoyo yathu.<br>2. Anthu awa onse anakhalapo pa mapazi a Yesu: Chitsanzo - ***Mateyu 28: 9, Marko 5: 22, Luka 7: 38, Luka 8: 35***. Onani mavesi amenewa ndipo pezani kuti anthu amenewa anali yani ndi kukambirana chomwe chinawachititsa kuti akhale pa mapazi a Yesu. | Gwiritsani ntchito Vesi Yoloweza kuti ikuthandizeni poonanso Phunziroli kuti muone:<br>1. Pali nthawi yoyenera kumvetsera Ambuye Yesu. ***(Marko 6: 31)***<br>2. Pali nthawi yoyenera kugwira ntchito ya Ambuye Yesu. ***(Marko 6: 7-13) (Aroma 12: 1)***<br>3. Ambuye alonjeza kudalitsa onse amene kutumikira kwawo kuchitika pamodzi ndi pemphero nthawi zonse. ***(Yohane 15: 5)*** |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kuphatikiza kupembedza ndi ntchito pa miyoyo yathu?<br>2. Kukhala moyo umene umabweretsa ulemu ndi chisangalalo?<br>3. Kukhala ndi mtima 'wotumukira bwino' m'malo 'motumikira kwambiri'?<br>4. Kuonetsetsa kuti ntchito sikutchinga kuwerenga Baibulo ndi nthawi ya pemphero?<br>5. Kuganiza za malo ndi ufulu umene Khristu akuyenera kukhala nazo m'mitima mwathu? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kuonetsetsa kuti tili ndi nthawi yoyenera yopemphera ndi kuphunzira Baibulo tsiku lililonse.<br>2. Kuonetsetsa kuti kutumikira kwathu Ambuye Yesu kusakhale ngati ntchito wamba, popanda kudzipereka kwa Iye. |

| | B3 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 2 – Betaniya<br>Mutu – Chisoni chisanduka chimwemwe! | B3 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 2 – Betaniya<br>Mutu – Pa manda |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 11: 1-7 ndi 17-44***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 11: 25***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ndi Ambuye Yesu wokha amene angaukitse munthu wakufa.<br>2. Ndi Ambuye Yesu wokha amene angapereke moyo wosatha kwa ochimwa, amene Paulo akunena kuti: ‘akufa chifukwa cha zolakwa zanu ndi machimo anu.’ ***(Aefeso 2: 1)*** | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 11: 1-44***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 11: 25-26***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kuukitsidwa kwa Lazaro ndi Ambuye Yesu inali njira yofunika yoonetsera mphamvu zake pa imfa ndi kuuka kwa akufa ndi chinthu chofunika kwambiri pa chikhulupiriro cha Chikhristu. Yesu sanali ndi mphamvu yokha yodziukitsa yekha ***(Yohane 10: 18)*** komanso youkitsa ena.<br>2. Yesu analira pa gulu ***(vesi 35)*** kuonetsa kuti amasamalira kwambiri za ife pamene tikudutsa m’mayesero ndi m’chisoni. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ophunzira kuti akumbukire zodabwitsa zina zimene Yesu anachita, ndipo kambiranani kuti muone kuti ndi chodabwitsa chiti chomwe ndi choposa zonse.<br>Ichi ndi chodabwitsa chomaliza mu utumiki wa pa gulu wa Ambuye Yesu. Ayuda ankafunsa kuti n’chifukwa chiyani Yesu analola kuti Lazaro amwalire popeza Iye ankatha kuchiza osaona. ***(vesi 37)*** Iye anachita zimenezi, koma poukitsa Lazaro kwa akufa, Iye ankaonetsa choonadi ndi mphamvu za mawu ake pa ***vesi 25***: ‘Ine ndine kuuka ndi moyo.’ | Yambani phunziro lino pofotokoza za kuukitsidwa kwa Lazaro kwa akufa, chodabwitsa chomaliza cha zodabwitsa zisanu ndi ziwiri za mu Uthenga Wabwino wa Yohane pofunika kutsimikizira Ayuda ambiri amene analipo kuti Iye anali Mwana wa Mulungu ndipo anamukhulupirira. ***(11: 45)*** Komabe, Ayuda ena amene anaonanso chodabwitsa ichi sanakhulupirire ndipo anapita kukawuza Afarisi zomwe zinachitika ku Betaniya. Mwina iwo ankafuna kupeza chifukwa chophera Ambuye Yesu. ***(11: 46)*** Langiza ophunzira kuti zinthu zili moteronso lero lino – Alipo amene amavomereza kuti Ambuye Yesu anali Mulungu ndipo ankachita zodabwitsa komanso alipo ena amene amakana zimenezi ndipo amatsutsa kuti Iye anachita zodabwitsa. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ku nyumba ya Mariya, Marita ndi Lazaro ndi imodzi mwa nyumba zimene Yesu ankakonda kupitako. Mutha kufunsa ophunzira ngati Ambuye Yesu ali m’nyumba zawo/m’mitima/m’miyoyo ***(Chivumbulutso 3: 20).***<br>2. Monga Ambuye Yesu anaukitsa Lazaro kuchoka ku imfa ndi kupita ku moyo, Iye atha kupereka kwa iwo amene ndi akufa ku uzimu moyo wauzimu watsopano umene ndi wamuyaya.<br>3. Nkhani iyi ikutionetsa kuti Ambuye Yesu ndi Mpulumutsi wachifundo; ‘Yesu analira’ ***(vesi 35)*** ndipo Ayuda amene anali pamenepo anadziwa momwe Iye ankakondera Lazaro. ***(vesi 36)*** Iye ankawakondanso koma ambiri sankazindikira.<br>4. Pamene Yesu anatulutsa Lazaro m’manda, anamupatsa moyo watsopano; ‘anamasulidwa’ nsalu za m’manda ***(vesi 44)*** ndipo anali mboni ya mphamvu ya Ambuye Yesu pa moyo wake.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 2.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Chisoni chisanduka chimwemwe! | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mariya ndi Marita anapita kwa Yesu kukapempha thandizo pamene mlongo wawo anamwalira chifukwa iwo anaona zodabwitsa zomwe ankachita. ***(11: 1-3)***<br>2. Yesu ankakonda banja limeneli koma sanayankhe msanga pempho lawo. Lazaro anamwalira kuti ophunzira ake ndi Ayuda ena amene analipo aone mphamvu yake pa imfa. ***(11: 5-6)***<br>3. Yesu analira chifukwa anakhudzika mu mtima ndi imfa ya Lazaro ***(11: 35)***<br>4. Yesu anayankhula kwa munthu wakufa ndipo wakufayo anamva ndi kuyankha! ***(11: 43-44)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 2.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Pa manda. |
| **KUKUMBUTSANA** | 1. Monga Lazaro anapatsidwa moyo watsopano ***(vesi 44-45)*** moteronso amene amakhulupirira Ambuye Yesu amapatsidwa moyo watsopano. Onani pa ***Akolose 2: 13*** ndi ***2 Timoteo 1: 10***, kuti muone mmene Ambuye Yesu amaperekera ‘moyo watsopano’ kwa ochimwa ‘akufa’.<br>2. Monga moyo watsopano wa Lazaro unali chizindikiro cha mphamvu ya Ambuye Yesu kugwira ntchito m’moyo wake, moterenso Ambuye Yesu amapereka kwa amene amakhulupirira mphamvu yokhala moyo mwa Iye. ***(Aefeso 2: 10)*** | Onaninso phunziroli pofananitsa ndi masautso a miyoyo yathu ndi kuonetsa momwe Ambuye Yesu angachitire kuti zinthu zikhale bwino. Werengani ***Aroma 8: 28***. Kuchedwa kwa Ambuye kutha kuoneka ngati kuti sakusamala za ife ndipo sakuyankha koma tikuyenera kuphunzira kufatsa ndi kumudalira nthawi zonse chifukwa sangatikhumudwitse. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Kodi taphunzira chiyani za kulapa ndi kutembenukira kwa Ambuye Yesu kuti ‘tikhale m’moyo watsopano’? ***(Aroma 6: 4)***<br>2. Kodi taphunzira chiyani za kumvera Mawu a Mulungu pogawana ndi ena Uthenga Wabwino, kukhala wophunzira wachidwi pa sukulu, kumvera makolo komanso mwina kubatizidwa? | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Akhristu ali ndi moyo wauzimu umene imfa singagonjetse kapena kuononga. Chitsimikizo chimenechi chitipanga ife kufuna kukhala moyo odzipereka kwa Ambuye Yesu. ***Afilipi 1: 21-23***.<br>2. Pa chodabwitsa ichi Ambuye Yesu akuonetsa kuti amasamalira kwambiri ndipo amalira nafe nthawi ya mavuto athu. |

| | **B3 – KALASI Lachitatu**<br>**Phunziro 3 – Betaniya**<br>**Mutu – Ulendo wina** | **B3 – KALASI Lachinayi**<br>**Phunziro 3 – Betaniya**<br>**Mutu – Pa chakudya** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 12: 1-11***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Yohane 4: 19***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pamene tikukondadi Ambuye Yesu, timapeza njira zomuthokozera.<br>2. Tisachedwe kuchita chomwe tingathe kuchita kwa Ambuye Yesu chifukwa sitidziwa kutalika kapena kuchepa kwa nthawi imene tili nayo yomutumikira. | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 11: 55-57; 12 :1-11***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Salimo 95: 6***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Palibe chinthu cha mtengowapatali chomwe sitingapereka kwa Ambuye Yesu Khristu. Iye akuyenera kulandira zabwino kwambiri kuchokera kwa ife!<br>2. Ngati timakonda Ambuye Yesu tidzakhala moyo womvera malangizo ake amene watipatsa, monga alili m'Chipangano Chatsopano. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani kuti Betaniya kunali ndi mbiri yabwino kwa Ambuye Yesu. Kumbutsani ophunzira kuti m'nyumba mwa Mariya ndi Marita, Ambuye Yesu anaphunzitsa kufunika kwa kupembedza. Mu phunziro 2 Yesu anaonetsa kuti anali 'Kuuka' pamene anaukitsa Lazaro kwa akufa. M'phunziro lino Ambuye Yesu ali pa chakudya m'nyumba ku Betaniya. | Nkhani imene ili pa ***Yohane 12: 1-11*** ndi yofanana ndi yomwe ili pa ***Marko 14: 3-9***. Ambuye Yesu akuyamikira Mariya chifukwa cha kusadzikonda kwake pa kupembedza pamene akudzoza mapazi ake ndi mafuta a mtengowapatali. Mafuta onunkhira ndi zokometsa zinali zofunika kwambiri pamene ankayika m'manda munthu wakufa – werengani pa ***Genesis 50: 2-3***. Yesu akuyankha za kudzipereka kwa Mariya pa ***vesi 7*** ponena kuti izi wachita pokonzera kuyikidwa m'manda kwake. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mariya, Marita ndi Lazaro anapatsidwa mwayi okhala pa chakudya ndi Ambuye Yesu, kudya pamodzi ndi kusangala ndi ubale wawo. ***(vesi 2)***<br>2. Mwayi umene anapatsidwa Mariya odzoza mapazi a Ambuye Yesu ndi mafuta a mtengowapatali ndi kupukuta mapazi ake ndi tsitsi lake ***(vesi 3)***, kutionetsa ife kuti palibe chinthu chofunika kwambiri kwa ife chimene sitingapereke kwa Iye pakuti Iye ndi woyenera zabwino zathu zonse.<br>3. Pamene Yudase anadandaula kuti akanatha kugulitsa mafutawo ndipo ndalama zake ndi kupereka kwa osauka ***(vesi 5)***, Ambuye Yesu anamukumbutsa kuti anthu osauka adzakhala m'dziko lapansi nthawi zonse amene anthu ena adzawathandiza. Koma, mwayi wogwiritsa ntchito mafuta amenewa pa Iye unali ochepa chifukwa ankapita kukafa pa mtanda chifukwa cha ochimwa.<br>4. Akulu a ansembe ankafuna kupha Lazaro ***(vesi 10)***. Izi zinali chomwechi chifukwa ankasutsa za kuuka kwa akufa ndipo ankafuna kupha Lazaro chifukwa unali umboni woti Ambuye Yesu ndi kuuka ndi moyo.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Ulendo wina. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. **Nyumba** - Bwerezani kuona kuti nyumba ku Betaniya ***(vesi 1)*** anali malo (i) wotumikira ndi malangizo; (ii) wopembedza ndi chiyanjano; ndi (iii) imfa ndi kuuka kwa akufa.<br>2. **Phwando *(vesi 2)*** linali 'la Iye'. Mariya, Marita ndi Lazaro anali zifukwa zokwanira kukumana naye monga mlendo wawo wamkulu.<br>3. **Kudzoza *(vesi 3)*** kunaonetsa kuti Mariya ankakonda Ambuye Yesu chifukwa chikondi chimaoneka kudzera mu kudzipereka kwa munthu.<br>4. **Kuyamikira *(vesi 7-8)*** kunali kwakulu kwambiri kuposa kumene Yudase anachitapo ndi Yesu akunena kuti kupembedza kotero kudzakhala chikumbutso mu mbiri ya mpingo – Werengani ***Mateyu 26: 13***.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Pa chakudya. |
| **KUKUMBUTSANA** | Nkhani yomweyi ikupezeka pa ***Marko 14: 3-9***. Werengani ***vesi 8*** kuti mupeze zomwe Ambuye anayankhula zokhudza mayi amene anadzoza mafuta mapazi ake.<br>Werengani nkhani yomweyi pa ***Mateyu 26: 6-13***, ndipo onani zomwe Ambuye Yesu anafotokoza zomwe zinayenera kuchitikiranso polalikira Uthenga Wabwino atafa, kuti zomwe anachita mayiyu zidzalalikidwenso ngati chikumbutso chake. | Funsani ana mafunso pamene mukuonanso Phunziro limeneli amene awathandize kuyankha molondola mafunso amene ali mu Phunziro 3. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi taphunzira chiyani za momwe chikondi chanu pa Ambuye Yesu chingalimbikitsire ena?<br>2. Ayuda ambiri anakhulupirira Ambuye Yesu ***(vesi 11)*** chifukwa anaona chizindikiro cha mphamvu yake pa moyo watsopano mwa Lazaro. Nanga inu mungalimbikitse ena motani ndi moyo wanu kuti akhulupirire Ambuye Yesu? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. **Nyumba** – Kodi Ambuye Yesu ali m'nyumba zathu monga mmene taonera pa 1 paja?<br>2. **Phwando** – Kwa Mkhristu, kodi Ambuye Yesu ndi woyamba m'miyoyo yathu?<br>3. **Kudzoza** – Kodi timakonda Ambuye Yesu motani? Kodi ndimamupatsa zabwino kwambiri?<br>4. **Kuyamikira** – Ambuye anayankhula za Mariya kuti anachita zomwe akanatha. ***(Marko 14: 8)*** |

| | B3 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 4 – Betaniya<br>Mutu – Ulendo wa ku Yerusalemu | B3 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 4 – Betaniya<br>Mutu – Ulendo wa ku Yerusalemu |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 19: 28-44***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 1: 12***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pamene Yesu ankalowa mu Yerusalemu, otsatira ake anayamba kuyimba, kumutamanda chifukwa cha ntchito zamphamvu zomwe anachita pakati pawo.<br>2. Yesu analirira mzinda wa Yerusalemu chifukwa anthu anamukana ndipo analibe malo ake pakati pawo. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 19: 28-44***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 1: 12***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. N'zofunika kwambiri kulandira Ambuye Yesu m'mtima mwathu ndi m'miyoyo yathu lero chifukwa tsiku lina nthawi idzakhala itatha kuti tikhale ndi mwayi otero.<br>2. Ambuye Yesu amasangalatsidwa kugwiritsa ntchito chikhulupiriro chathu, chikondi chathu, kupembedza kwathu ndi katundu wathu kuti Iye alandire ulemu ndi ulemerero kuchokera kwa ife anthu ake. |
| MAWU OYAMBA | Fotokozani za mwambo wa "Kanjedza" kuti sunachitike mwa mwayi. Ananeneratu zaka za m'mbuyomo.<br>Werengani ***Zekariya 9: 9*** pamene analemba za kulowa mwachipambano kwa Ambuye Yesu zaka 500 zapitazo zisanachitike. | Yambani phunziroli ndi kufotokoza kuti Ambuye Yesu analirira Yerusalemu ***(vesi 41-42)*** chifukwa anataya mwayi wake womulandira Iye monga Mesiya zomwe zikanabweretsa mtendere. Apa n'kuti nthawi itatha ndipo Ambuye Yesu akuchenjeza zotsatira zowawa zimene zikubwera m'tsogolo pa dziko la Ayuda.<br>Monga mmene Ambuye Yesu analosera m'chaka cha 30 AD, ***(Luka 19: 43-44)*** mkulu wa asilikali a Chiroma, Tito, anathira nkhondo Yerusalemu (AD 70) ndi kugwetsa Nyumba ya Mulungu komanso kupha anthu anali m'menemo. Ambuye Yesu anapita ku Yerusalemu ndi cholinga chofuna kupereka chipulumutso koma iwo sanafune kumulandira choncho masautso anadzawagwera. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kulowa mwachipambano ***(vesi 28-40)*** kwa Ambuye Yesu poyamba pa sabata ya kupachikidwa kwake.<br>2. Ophunzira ake anayamba kuyimba motamanda ***(vesi 37)***. Onani ankafuula kuti "mtendere Kumwamba" osati "mtendere pa dziko lapansi" chifukwa imfa ya Ambuye Yesu ndi kuuka kwake kunali kobweretsa "mtendere Kumwamba" padzakhala popanda "mtendere pa dziko lapansi" chifukwa anali pafupi kupha Ambuye Yesu – mfumu ya mtendere.<br>3. Yesu analirira Yerusalemu chifukwa anthu ake akumukana Iye ndipo apa nthawi inali itatha iwo anataya mwayi wawo. ***(vesi 42)***<br>4. Yesu akulosera kuti m'chaka cha AD 70, pansi pa ulamuliro wa Tito, mkulu wa ankhondo wa Chiroma, Yerusalemu ndi anthu ake adzaonongedwa chifukwa 'sanazindikire nthawi ya kubwera kwake' ***(vesi 44)***, kutanthauza kuti Ambuye anawapatsa chipulumutso koma iwo sanachifune.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Ulendo wa ku Yerusalemu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. **Kulowa mu Yerusalemu** – Ambuye Yesu analowa mu Yerusalemu pa mwana wa bulu wobwereka, monga mmene ananenera pa ***Zekariya 9: 9***. Iwo amene anaona mdipiti wachipambano wa Yesu polowa mu Yerusalemu anazindikira kuti Yesu ndiye amene anakwaniritsa ulosi umene unayankhula zaka 500 za m'mbuyomo zisanachitike. ***(Luka 19: 35-36)***<br>2. **Nthawi Yolowa mu Yerusalemu** – Yesu anasankha nthawi imene Aisrayeli onse anasonkhana mu Yerusalemu pa Phwando la Paskha.<br>3. **Chiyembekezo cha Anthu** – Anthu ankatamanda Mulungu chifukwa chowapatsa mfumu amene ankamuyembekezera kukhala mtsogoleri wa dziko. Koma pamene anazindikira kuti Iye anabwera kudzakhazikitsa ufumu wamuyaya, anamuukira. ***(Luka 19: 38)***<br>4. ***Machitidwe a Afarisi*** – Afarisi anatsutsana ndi zomuyamikira Yesu pagulu ndipo anapempha Yesu kuti alamule anthu kuti akhale chete, koma Yesu anawadzudzula powawauza kuti mitima yawo ndi yowuma ngati miyala! ***(Luka 19: 39-40)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Ulendo wa ku Yerusalemu. |
| KUKUMBUTSANA | Onaninso nkhaniyo ndipo kambiranani za kufunika kwa kukhulupirira Ambuye Yesu monga Mpulumutsi tsopano. Onani ***2 Akorinto 6: 2***. Mwina mawa nthawi idzakhala itatha. Komanso ganizirani za chiweruzo chimene chikubwera pa dziko lapansi, monga nthawi ya ulamuliro wa Tito mu AD 70, ndipo amene alibe Ambuye Yesu adzatayika. | Onaninso Phunziroli pofotokoza tsatanetsatane wa zonse zochitika pa moyo wa Yesu. Yerusalemu linali likulu la chipembedzo ndi ndale komanso kwawo kwa Ayuda ndi Bwanamkubwa wa Chiroma. Zochitika zofunika kwambiri pa moyo wa Yesu zinachitikira mu Yerusalemu kuphatikiza kupachikidwa ndi kuuka kwake. Sabata lake lomaliza pa dziko lapansi anali mu Yerusalemu. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ganizirani za tanthauzo la kuchoka ku tchimo ndi kukhulupirira Ambuye Yesu kuti tipulumuke.<br>2. Vesi Yoloweza ikunena za amene analandira Ambuye Yesu kuti ndi: 'ana a Mulungu.' Ganiziranso mayina ena amene analandira Ambuye Yesu amatchedwa (monga, Mkhristu, ndi ena). | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Moyo wosatha ulipobe kwa amene amaulandira pamene nthawi ilipo.<br>2. Ganizira njira zomwe Ambuye angafune kugwiritsa ntchito miyoyo yathu monga pa ***Luka 19: 31***.<br>3. Monga mmene ulosi wa pa ***Zekariya 9: 9*** unakwaniritsidwa, ulosi wa Kubwera Kwachiwiri kwa Ambuye Yesu udzakwaniritsidwanso. |

| | **B4 – KALASI Lachitatu**<br>**Phunziro 1 – Ambuye Yesu**<br>**Mutu – ‘Kufa’** | **B4 – KALASI Lachinayi**<br>**Phunziro 1 – Ambuye Yesu**<br>**Mutu – Imfa yake** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 23: 1-26 ndi 32-46***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 23: 33***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anafa kuti tikhululukidwe machimo athu.<br>2. Kuti tikafike Kumwamba tikuyenera kutembenuka mtima ndi kukhulupirira Ambuye Yesu. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 23: 32-56***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 15: 13-14***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kuti tidzapite Kumwamba tikuyenera kuvomereza kuti ndife ochimwa, oyenera kulangidwa ndi Mulungu.<br>2. Kenaka tikuyenera kukhulupirira Ambuye Yesu kuti analibe tchimo ndipo analangidwa m’malo mwathu. |
| **MAWU OYAMBA** | Yambani phunziroli pofunsa ophunzira zimene akudziwa za kufunika kwa Paskha. Fotokozani kuti phunziro ili likufotokoza za Paskha yoyamba. Kambiranani momwe phunziro ili likuonetsera kuti si anthu onse amene akupita Kumwamba. Achifwamba awiri anapachikidwanso pa mtanda pamodzi ndi Ambuye Yesu; mmodzi anapita Kumwamba pamene wina sanapite. | Mwachidule fotokozani zomwe zinachitika mpaka pa mtanda, kuphatikiza kugwidwa kwake, milandu yake ndi kuyenda kupita ku Kalvari. Kambiranani momwe phunziro ili lifotokozera kuti chipulumutso chakhazikika pa kutembenuka mtima ndi chikhulupiriro ndi momwe wachifwamba wolapa uja anapitira Kumwamba pamene wosalapa wina uja sanapite. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Pilato sanapeze cholakwa chilichonse mwa Yesu, komabe anaweruza kuti aphedwe pofuna kusangalatsa anthu. ***(vesi 1-7, 13-25)***<br>2. Ngakhale Pilato ndi Herode ankadana, anakhala abwenzi ndipo onse anali mbali imodzi, yotsutsana ndi Ambuye Yesu. ***(vesi 12)***<br>3. Ora lachisanu ndi chimodzi (9 m’mawa - 3 madzulo) – Yesu anali pa mtanda wa pakati pa achifwamba awiri pofuna kukwaniritsa mawu amene ali pa ***Yesaya 53: 12***.<br>4. Panali achifwamba awiri ***(vesi 39-43)*** koma mmodzi yekha ndiye anapita Kumwamba. Onani zomwe zili pa ***vesi 43***: ‘lero’ – kufulumiratu! - ‘ndi Ine’ – kukhala naye pamodzi! ‘Ku paradizo’ – chisangalalo!<br>5. Maora atatu a mdima ***(vesi 44-46)*** ndipo nsalu yotchinga m’Nyumba ya Mulungu inang’ambika pakati, kusonyeza Ambuye Yesu ndi njira ya kwa Mulungu. ***(Ahebri 10: 19-20)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – ‘Kufa’. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Maora asanu ndi limodzi opachikidwa ankakwaniritsa za pa ***Yesaya 53: 12*** - (9 m’mawa – 3 madzulo).<br>2. Nkhani ya kulapa kwa wachifwamba ***(23: 42-43)*** ikuonetsa chipulumutso chomwe chimabwera ndi kutembenuka mtima ndi chikhulupiriro chokha. Munthu uyu anapita Kumwamba koma anali asanabatizidwe kapenanso kuchita nawo masakamenti.<br>3. Achifwamba awiriwa akuyimira magulu awiri a anthu – amene amakonda Ambuye Yesu ndi amene ndi adani ake.<br>4. Pa maora atatu a mdima, ***(vesi 44-46)*** Yesu analangidwa chifukwa cha machimo athu ndipo kudzera mu imfa yake njira yopita pamaso pa Mulungu inatsekuka kwa onse amene amapita kwa Iye mwachikhulupiriro.<br>5. Nkhaniyi ikutionetsa ***(vesi 50-56)*** kuti Yosefe, wophunzira wake mwamseri, anali bwenzi lake lenileni la Ambuye Yesu monga amayi aja okhulupirika amene atchulidwa. Izi zikuoneka kudzera mu ulemu umene anayikira m’manda Ambuye Yesu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Imfa yake. |
| **KUKUMBUTSANA** | Onaninso Phunziro popempha ophunzira kuti awerenge ***Yesaya 53: 12*** zomwe analemba zaka 700 Ambuye Yesu asanafe ndi kufotokoza kuuziridwa kwa Baibulo.<br>M’magulu lembani mutu wa nkhani yofotokoza za mtanda. | Onaninso phunziroli pofunsa ophunzira kuti awerenge ***Yesaya 53*** zimene zinalembedwa zaka 700 Ambuye Yesu asanafe ndi kukambirana momwe zikufananira ndi zomwe zili pa ***Luka 23: 32-56***. Zimene zikutsindika za kuuziridwa kwa Baibulo. M’magulu lembani maulosi ena amene atchulidwa pa ***Yesaya 53*** amene anakwaniritsidwa pa mtanda. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Tingatsimikize bwanji kuti machimo athu akhululukidwa?<br>2. Tonse timakumana ndi vuto losankha mbali imene tikufuna kukhala – mbali ya amene amakonda Ambuye Yesu kapena ya amene ndi adani ake.<br>3. Kodi mungayankhe chiyani munthu amene akunena kuti tonse tidzapita Kumwamba? | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Tonse timakumana ndi nthawi yofuna kusankha kukhala bwenzi kapena mdani wa Yesu.<br>2. Ngati timakonda Ambuye Yesu, monga Yosefe, tidzapeza njira zosonyezera chikondi. Kodi tingachionetse motani?<br>3. Kodi mungayankhe chiyani munthu amene akunena kuti tonse tidzapita Kumwamba? |

| | B4 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 2 – Ambuye Yesu<br>Mutu – 'Kuuka' | B4 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 2 – Ambuye Yesu<br>Mutu – Kuuka kwake kwa akufa |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 20: 1-18***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aroma 10: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ambuye Yesu atatha masiku atatu ali m'manda anauka kwa akufa.<br>2. Mariya wa ku Magadala anaonetsa chikondi chake kwa Ambuye Yesu Khristu. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 8: 1-3, Yohane 20: 1-18***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aroma 10: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ambuye Yesu anagonjetsa imfa pamene anaukananso.<br>2. Mariya wa ku Magadala anali wotsatira wa Ambuye Yesu wodzipereka kwambiri.<br>3. Kudziwa kuti kuukitsidwa ndi chinthu chenicheni ndipo chili ndi maumboni ambiri m'Baibulo. |
| MAWU OYAMBA | Kambiranani tanthauzo la 'kuuka kwa akufa' ndipo funsani ophunzira kuti atchule mayina a anthu amene Ambuye Yesu anawaukitsa kwa akufa (Lazaro – ***Yohane 11: 44***, mwana wamkazi wa Yairo – ***Luka 8: 55***). Dziwani kuti mphamvu ya kuukitsa ndi ya Ambuye Yesu. | Kambiranani za kuti mphamvu ya kuuka kwa akufa ili ndi Ambuye Yesu ndipo pezani anthu amene anawaukitsa kwa akufa. (Lazaro – ***Yohane 11: 44***, mwana wamkazi wa Yairo - ***Luka 8: 55***). Ndiponso fotokozani kuti amene akumwalira ali mwa Ambuye Yesu adzaukitsidwa m'tsogolo. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mariya wa ku Magadala, Petro ndi Yohane anaona chizindikiro choti Ambuye Yesu wauka – manda wopanda kanthu. ***(Yohane 20 :1-8)***<br>2. Petro ndi Yohane anabwerera kupita kwawo koma Mariya wa ku Magadala anatsatirira pa khomo la manda. ***(Yohane 20: 10-18)***<br>3. Ambuye Yesu anamupatsa mphotho ya kudzipereka kwake pomuonekera ndi kumufotokozera kuti akapita Kumwamba, Iye adzatumiza Mzimu Woyera amene adzakhale m'mtima ya okhulupirira.<br>4. Iye akumutuma kuti apite akawuza ophunzira ake kuti ali moyo ndipo akakumane nawo ku Galileya. ***(Mateyu 28: 10)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 2.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – 'Kuuka'. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mariya wa ku Magadala ankatumikira Ambuye Yesu ali pa dziko lapansi ndipo anaonetsa kudzipereka kwake pokhala woyamba kuona manda wopanda kanthu. ***(Luka 8: 1-3)***<br>2. Mariya wa ku Magadala, Petro ndi Yohane anaona chizindikiro cha kuuka kwa akufa, ndipo anaona momwe zofuna za ku manda zinalili m'mandamo - kusonyeza kuti kuchoka kwa Ambuye kunali mwadongosolo ndi mosafulumira, kutsutsa maganizo akuti mtembo wake unachita kubedwa. ***(Yohane 20: 3-9)***<br>3. Ambuye Yesu anamupatsa mphotho ya kudzipereka kwake pomuonekera ndi kumufotokozera kuti akapita Kumwamba, Iye adzatumiza Mzimu Woyera amene adzakhale m'mtima ya okhulupirira. ***(Yohane 20: 10-18)***<br>4. Iye akumuwuza kuti apite akawuza ophunzira ake kuti ali moyo ndipo akakumane nawo ku Galileya. ***(Mateyu 28: 10)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 2.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuuka kwake kwa akufa. |
| KUKUMBUTSANA | Lumikizani phunziro ili ndi ndime zochokera m'Chipangano Chatsopano pamene Ambuye Yesu akuneneratu za kuuka kwake kwa akufa. Kambiranani kufunika ndi kupambana kwa kuuka kwa akufa.<br>***• Mateyu 16: 21; 17: 22-23; 20 :18-19***<br>***• Luka 18: 31-33; 24: 7***<br>***• 1 Akorinto 15: 3-4*** | Lumikizani phunziroli ndi ***1 Akorinto 15: 3-8, 12-20*** ndi kuonetsa vesi 4 kuti ndi zomwe zili pa ***Yesaya 53: 9*** ndi ***Salimo 16: 9-10.***<br>Kambiranani za anthu osiyanasiyana amene anaona Ambuye Yesu atauka kwa akufa ***(1 Akorinto 15: 5-8)*** ndi kufunika kwake kwa kuuka kwa akufa ***(1 Akorinto 15: 17)***. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kufunika koti ophunzira anene kuti amakonda Ambuye Yesu monga Mpulumutsi wawo.<br>2. Kuganizira momwe chikondi chathu pa Iye chikukhudzira miyoyo yathu.<br>3. N'koyenera kuphunzira kuchokera m'phunziro limeneli kuti kuukitsidwa kudzachitikadi. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ganizirani kufuna kwa ubale ndi chikondi pa Ambuye Yesu.<br>2. Kuuka kwa akufa ndi chinthu chofunika kwambiri pa chikhulupiriro cha Chikhristu chifukwa Khristu akanapanda kuuka kwa akufa, imfa yake ikanakhala yopanda phindu ndipo ife sitikanakhala ndi chiyembekezo chokhala Kumwamba tsiku lina kwamuyaya. |

| | B4 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 3 – Ambuye Yesu<br>Mutu – 'Kupita' | B4 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 3 – Ambuye Yesu<br>Mutu – Kupita Kumwamba |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 20: 19-31, Luka 24: 45-53***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 24: 51***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ambuye Yesu akatiwuza kanthu kudzera m'Baibulo, timamukondweretsa tikamvera.<br>2. Cholinga cha Uthenga Wabwino wa Yohane ndi chakuti iwo amene akuwerenga akhulupirire ndi kukhala ndi moyo wosatha. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 24: 45-53, Machitidwe 1: 1-12***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 24: 51***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ambuye Yesu akufuna amene ndi ake kuti akhale mboni zake pa dziko lapansi.<br>2. Tsiku lina Ambuye Yesu akubweranso pa dziko lapansi kudzatenga ake kupita nawo Kumwamba. |
| MAWU OYAMBA | Kambiranani, ndi zitsanzo zoyenera, momwe timakhulupirira zinthu zambiri zomwe sitinazionepo kapena kuzikhudza. Fotokozani kuti chikhulupiriro cha Chikhristu sichili pa zooneka ndi maso koma kukhulupirira Mawu a Mulungu ndi Ambuye Yesu. | Kambiranani momwe timasungira mawu omaliza a munthu amene timamukonda, makamaka ali pafupi kumwalira. Ganizani mawu amene ayankhula anthu otchuka akumwalira m'mbiri ya dziko lapansi. Fananitsani ndi mawu otsiriza a Ambuye Yesu. ***(Machitidwe 1: 8-9)*** |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kambiranani za kuonekera kwa Yesu kwa ophunzira ake ndipo ikani chidwi pa mawu ake akuti: "Mtendere ukhale nanu." ***(vesi 21)*** Fotokozani kuti, chifukwa cha imfa ya Yesu, amene amakhulupirira amakhala ndi mtendere weniweni. ***(Aroma 5: 1)***<br>2. Yesu akuyankhula ndi Tomasi wokayika ndi kumutsimikizira kuti Iye ndi Khristu amene wauka kwa akufa. ***(Yohane 20: 27- 28)***<br>3. Tomasi akuyankha ndi mawu achikhulupiriro ndi kudzipereka.<br>4. Ambuye Yesu anachoka ndi kupita Kumwamba patatha masiku makumi anayi atauka kwa akufa kuchokera pa Phiri la Azitona ndipo ophunzira ake anabwerera ku Nyumba ya Mulungu akutamanda ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha kuuka kwake komanso kuti adzabweranso. ***(Luka 24: 50-53)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – 'Kupita'. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ambuye Yesu analamula ophunzira ake kuti akhale mboni zake ***(Machitidwe 1: 8)*** kuyambira mu Yerusalemu, m'dziko la Israyeli ndi ku dziko lonse lapansi.<br>2. Ambuye Yesu anakwera Kumwamba kuchokera pa Phiri la Azitona ***(Machitidwe 1: 12)*** ndipo adzabweranso pa Phiri la Azitona ***(Zekariya 14: 4).***<br>3. Iye anakwera Kumwamba m'thupi ndi onse akumuona. Tsiku lina adzabweranso m'thupi ***(Malaki 3: 1)*** onse akumuona ***(Mateyu 24: 30)***.<br>4. Iye anabisika m'mitambo mwamphamvu ndi ulemerero ndipo adzabweranso kuchokera Kumwamba mwaphamvu ndi ulemerero. ***(Mateyu 24: 30)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kupita Kumwamba. |
| KUKUMBUTSANA | Phunzirani Vesi Yoloweza ndipo kambiranani momwe ikufotokozera zonse za m'phunziroli. Kumbutsani ophunzira kuti ophunzira ankayembekezera kukwaniritsidwa kwa lonjezo la kubwera kwa Mzimu Woyera. ***(Luka 24: 49)*** | Onani m'Baibulo ndime zofotokoza mfundo 1-4 zomwe zili m'mwambazi ndipo fananitsani ndi kusiyanitsa Kukwera kwa Ambuye Kumwamba ndi za Kubweranso Kwachiwiri pa dziko lapansi. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi tingakhulupirire bwanji Ambuye Yesu kuti atipulumutse ngakhale sitinamuone?<br>2. Ambuye Yesu analimbikitsa ophunzira ake kuti azimutumikira Iye akapita Kumwamba. Kodi ife lero tingamugwirire ntchito yotani?<br>3. Onani pa ***Machitidwe 1: 8***. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Momwe okhulupirira Ambuye amachitira umboni ku nyumba zawo, ku sukulu ndi pakati pa anzawo.<br>2. Ganizani anthu amene anachoka kwawo kupita ku mayiko ena kukakhala mamishoni.<br>3. Ophunzira afotokoze momwe anakhulupirira Yesu kukhala Mpulumutsi wawo ndi Ambuye. |

| | **B4 – KALASI Lachitatu**<br>**Phunziro 4 – Ambuye Yesu**<br>**Mutu – ‘Kubwerera’** | **B4 – KALASI Lachinayi**<br>**Phunziro 4 – Ambuye Yesu**<br>**Mutu – Kubwera kwake kwachiwiri** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 1: 4, 8-12***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 1: 11***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mphamvu ya Mzimu Woyera ndi yofunika pamene tikuchitira umboni kapena kulalikira Uthenga Wabwino.<br>2. Ambuye Yesu amene anakwera Kumwamba, adzabweranso pa dziko lapansi kudzatenga amene ndi okonzeka kukhala naye Kumwamba. | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 14: 1-6, Machitidwe 1: 9-11***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Atesalonika 4: 16-17***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kubwera Kwachiwiri kwa Ambuye pa dziko lapansi ndi chinthu chimene chidzachitikadi ngakhale tsiku ndi nthawi sizikudziwika.<br>2. Kubwera Kwachiwiri, akufa mwa Khristu adzaukitsidwa ndi kupita nawo Kumwamba pamodzi ndi Akhristu amene ali moyo. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani za mboni ya ngozi, amene anaona ndi kumva zomwe zinachitika. Ophunzira ankayenera kuyankhula zomwe Ambuye Yesu anachita iwo akuona. Ganizaninso za mphamvu zomwe ophunzira analandira kuti ziwathandize kukhala mboni za Ambuye Yesu, mphamvu zomwe ifenso timalandira pamene talapa tchimo lathu ndi kukhulupirira zomwe Ambuye Yesu anatichitira pa mtanda pochotsa machimo athu. Ifenso tikuyenera kukhala mboni. | Kumbutsani ophunzira kuti maulosi onse a m’Chipangano Chakale okhudza kubwera kwa Ambuye pa dziko lapansi ngati munthu anakwaniritsidwa, moteronso maulosi onse onena za Kubwera kwake Kwachiwiri.<br>Kambiranani ndi ophunzira kuti aliyense amafuna wokondedwa wake amene anachoka atabweranso, momwenso amene amakhulupirira Yesu akuyenera kuyembekezera kubweranso kwake. Onani pa ***Tito 2: 13***. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ambuye analamula ophunzira ake kuti akhale mboni zake kuyambira mu Yerusalemu, kenaka m’dziko la Israyeli, potsiriza ku dziko lonse lapansi. ***(Machitidwe 1: 8***)<br>2. ‘Amuna awiri atavala zonyezimira’ amene amayi anabwera ku manda anakumana nawo ***(Luka 24: 4)***, anawauza kuti m’manda munalibe munthu chifukwa Ambuye Yesu anali atauka kwa akufa. Mwina anali angelo omwewo, owoneka ngati anthu, amene ankauza ophunzira za Kubwera Kwachiwiri. ***(Machitidwe 1: 10-11)***<br>3. Kubwera kwake kudzafanana ndi Kukwera kwake.<br>4. Nthawi ya Kubwera Kwachiwiri sikudziwika, choncho n’kofunika kukhala okonzeka. ***(Machitidwe 1: 7)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – ‘Kubwerera’. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. ‘Amuna awiri amene anavala zoyera’ ***(Machitidwe 1: 10-11)*** anawuza ophunzira za Kubwera Kwachiwiri kwa Ambuye pa dziko lapansi. Lumikizani kuti muone kuti ndi angelo omwe pa ***Luka 24: 4*** amene anawuza amayi pa manda za kuuka kwa akufa.<br>2. Fananitsani lonjezo la Ambuye pa ***Yohane 14: 3*** ndi ***Machitidwe 1: 11*** ndipo fotokozani kulondola ndi kulimbikitsa kwa Malemba.<br>3. Werengani ***1 Atesalonika 4: 16-17*** ndi kufotokoza vumbulutso lozama la Paulo pa Kubwera Kwachiwiri. Fotokozani motere:<br>Pali phokoso lomwe lidzamveke – mfuwu ndi lipenga;<br>Zomwe tidzaone – Ambuye mwini;<br>Chodabwitsa chomwe tidzamve – kukwatulidwa;<br>Msonkhano wosangalatsa – ‘kukumana ndi Ambuye mlengalenga’;<br>Ndi chitonthoza – ‘kukhala ndi Ambuye’ kwamuyaya.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kubwera kwake kwachiwiri. |
| **KUKUMBUTSANA** | Onani mavesi otsatirawa kuti muone kuti Ambuye anayankhula za kubwera kwake ‘ngati mbala usiku’ chifukwa palibe amene amadziwa nthawi imene mbala ikubwera. N’chifukwa chake tikuyenera kukhulupirira Iye kuti tipumulutsidwe ndi kukonzekera kubweranso kwake. ***Mateyu 24: 44, Luka 12: 20.*** | Kubwera Kwachiwiri sikochititsa mantha kwa amene anapulumutsidwa ndipo ndi okonzeka kukumana naye. Baibulo limaphunzitsa kuti Akhristu akuyenera kuyembekezera kuonekera kwake ndi kumakhala moyo okondweretsa Iye. Onani pa ***Tito 2: 11-14 ndi 1 Yohane 3: 2-3.*** |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Aliyense akuyenera kumalingalira ngati ali okonzeka kupita Kumwamba, ngati Ambuye atabwera lero.<br>2. Kodi mungamuyankhe chiyani munthu amene anganene kuti nthawi ilipo yambiri yoti munthu n’kukhala wokonzeka kupita Kumwamba, kuchokera pa zimene mwaphunzira za Kubweranso Kwachiwiri?<br>3. Kodi nthawi yabwino kukonzekera kupita Kumwamba ndi iti? Onani pa ***2 Akorinto 6: 2***. | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Akhristu akuyenera kukhala moyo olungama poganizira kuti Ambuye ali pafupi kubweranso ndi kuti iwo adzapezeke ali mwa Iye akamadzabwera. Kodi izi zikutanthauza chiyani?<br>2. Osakhulupirira adzatsala Iye akadzabwera kachiwiri. Kodi choonadi chimenechi chikutiphunzitsa chiyani ife monga Akhristu, pa nkhani ya kuwachitira umboni? |

| | B5 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 1 – Antchito a Ambuye<br>Mutu – Kukonzedwa ndi Mulungu! | B5 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 1 – Akhristu Oyambirira<br>Mutu – Stefano |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 1: 7-9; 2: 1-13***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 14: 16-17***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Masiku oyambirira a Mpingo wa Chikhristu, Ambuye analamula ophunzira kuti apite akalalikire Uthenga Wabwino ku dera kwawo ndi ku dziko lonse lapansi.<br>2. Monga mmene Mzimu Woyera anabwera ndi kukhala m'mitima ya atumwi, moteronso amene amakhulupirira Ambuye Yesu adzakhala ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu yake kuti iwathandize kukhala miyoyo ya Chikhristu. | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 6: 1-15; 7: 54-60***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 6: 8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ndi anthu okhala ngati Stefano amene Mulungu amasintha dziko lapansi kudzera mwa iwo.<br>2. Ndi okhulupirira enieni, monga Stefano, amene amatsimikiza mtima kulalikira choonadi cha Uthenga Wabwino ndipo amakhudzidwa ndi zimene zimakondweretsa Mulungu, osati zomwe anthu amawanena kapena kuwachitira. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ophunzira kuti aganize momwe zinalili ndi ophunzira, Yesu atakwera Kumwamba, ndi pamene Mzimu Woyera anabwera pa tsiku la Pentekoste. Fotokozani nkhani ziwiri zomwe zikupezeka m'Machitidwe a Atumwi:<br>1. Ambuye Yesu tsopano atakwera Kumwamba akugwira ntchito kudzera mwa amene anali pa dziko lapansi amene anamukhulupirira kudzera mwa Mzimu Woyera.<br>2. Kuukitsidwa ndi kukwezedwa kwa Ambuye Yesu Kumwamba ndiye linali tsinde la uthenga uwu pamene unkalemba buku ili (60-67 AD). | Kambiranani za tanthauzo la masautso ndipo perekani zitsanzo za masautso a masiku ano.<br>Fotokozani kuti masiku oyamba a Chikhristu, atsogoleri achipembedzo anali ndi mphamvu zoyendetsa boma ndipo Akhristu nawo anali okonzeka kutsutsana nawo koma mwaulemu. Akhristu ankalemekeza ndi kumvera atsogoleri a dziko a nthawi imeneyo pokhapokha ngati malamulo a dziko ankatsutsana ndi Malamulo a Mulungu. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Vesi yofunika m'buku limeneli ndi ***Machitidwe 1: 8***, ndipo buku lonse la Machitidwe lawumbika pa nkhani imeneyi molingana ndi madera amene kunafalikira Uthenga Wabwino:<br>Mboni zanga mu Yerusalemu – ***Chaputala 1-7;***<br>Mboni zanga ku Yudeya – ***Chaputala 8: 1-4;***<br>Mboni zanga ku Samariya – ***Chaputala 8: 5-25;***<br>Mboni zanga ku Dziko lonse lapansi – ***Chaputala 8: 26***<br>2. Tsiku la Pentekoste ***(2: 1)*** ndi tsiku limene Mzimu Woyera anabwera kudzakhazikika mwa okhulupirira – Iye anabwera kudzakhala. Iwo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ***(2: 4)***. Pamene takhulupirira Ambuye Yesu, Mzimu Woyera amabwera kudzakhala mwa ife koma kuti tidzazidwe ndi Mzimu Woyera, tikuyenera kuwerenga Baibulo, kukhala ndi nthawi yopemphera ndi kukhala moyo womvera Ambuye.<br>3. Ambuye Yesu anayika maziko olimba pa ntchito imene anatsiriza pa mtanda ndipo tsopano akupereka mphamvu kwa okhulupirira kudzera mwa Mzimu Woyera, kuti akhale mboni ndi othandiza kufalitsa Nkhani Yabwino ya imfa yake, kuuka kwake ndi uthenga wa chipulumutso kwa onse. Mzimu Woyera akutchedwa kuti ndi 'Nkhoswe' pa Vesi Yoloweza ***Yohane 14: 16***, kusonyeza kuti Ambuye Yesu ndi Nkhoswe yathu kapena Mthandizi wathu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukonzedwa ndi Mulungu! | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Stefano anali ndi makhalidwe amene akuyenera kukhala m'moyo wa Mkhristu - mbiri yabwino, odzazidwa ndi Mzimu Woyera, odzazidwa ndi chikhulupiriro ndi mphamvu, nzeru ndi khumbo lofuna kutumikira Ambuye Yesu. ***(Onani Machitidwe 6: 3,5 ndi 8.)***<br>2. Kutsutsana ndi utumiki wamphamvu wa Stefano kunayambika pakati pa magulu a Ayuda amene anali ndi masunagoge mu Yerusalemu ndi madera ozungulira. Koma pamene Stefana ankaonekera pamaso pa Bwalo Lalikulu la Ayuda, anamva maumboni abodza ambiri otsutsa Stefano; ndipo iwo anaona ulemerero wa Ambuye Yesu pa nkhope ya Stefano ***(Machitidwe 6: 15)***. Stefano anadziteteza ndi mawu amphamvu ***(Machitidwe 7: 1-53)*** ndi kudzudzula kwambiri atsogoleri a Ayuda, ponena kuti akukana Mzimu Woyera ndi kuti ndi iwo amene anapachika Ambuye Yesu.<br>3. Mwina Stefano ankadziwa kuti moyo wake unali pachiopsezo koma anali wokonzeka kufa m'malo mokhumudwitsa Ambuye ake. Iye atangoyankhula zoti akuona 'Kumwamba kotsekuka' ***(Machitidwe 7: 56)*** gulu la anthu linamugwira ndi kupita naye kunja kwa mzinda ndi kumupha pomugenda miyala ***(Machitidwe 7: 57-58)***.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Stefano. |
| **KUKUMBUTSANA** | Dokotala Luka, mlembi wa Machitidwe a Atumwi, akuyamba ndi mawu akuti, 'zonse zimene Yesu anayamba kuchita ndi kuphunzitsa' pa ***Machitidwe 1: 1***. Pa ***Machitidwe 28: 31*** Paulo akulalikirabe nkhani yabwino ya Uthenga Wabwino. Dziwani kuti 'Buku la Machitidwe likupitirira - ntchito yofalitsa uthenga singathe mpaka Ambuye akabweranso kudzatenga amene amamukhulupirira.' | Kambiranani momwe mavesi awa akufotokozera zonse za m'phunziroli:<br>1. ***2 Timoteo 2: 3*** – "Umve nane zowawa, monga msilikali wa Khristu Yesu."<br>2. ***1 Petro 4: 14*** - "Ngati akuchitani chipongwe chifukwa cha dzina la Khristu, ndinu odala, ndiye kuti Mzimu waulemerero wa Mulungu uli pa inu." |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga okhulupirira Mzimu Woyera amakhala mwa ife. Ndi udindo wathu 'kudzazidwa ndi Mzimu'. Werengani ***Aefeso 5: 18***.<br>2. Kukhala ndi Nthawiyabaibulo idzakulimbikitsani: Kuwerenga Baibulo ndi Kupemphera. Tengani zomwe mukuwerenga ndipo motsogozedwa ndi Ambuye muzichita zimenezo pa moyo wanu wa tsiku ndi tsiku. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga Stefano anaphedwa chifukwa cha chikhulupiriro chake pa imfa ndi kuuka kwa Ambuye Yesu, moteronso Akhristu ambiri akuzunzidwa ngakhalenso kuphedwa m'mayiko ena lero chifukwa cha zikhulupiriro zimenezi.<br>2. Tikuyenera kupempha Ambuye Yesu m'mapemphero athu kuti atisunge kukhala odzipereka ndi okhulupirika posatengera zomwe tikukumana nazo m'miyoyo yathu. |

**B5 – KALASI Lachitatu**
**Phunziro 2 – Antchito a Ambuye**
**Mutu – Kukonzeka kufa!**

**B5 – KALASI Lachinayi**
**Phunziro 2 – Akhristu Oyambirira**
**Mutu – Filipo**

---

**Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 6: 1-5, 8-15; 7: 54-60***
**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 5: 44***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Stefano anali wokhulupirika pa zinthu zazing'ono asanayambe kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu, monga kutumikira pa nthawi ya chakudya ***(Machitidwe 6: 2)***, asanayambe kuchita zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa ***(Machitidwe 6: 8)***.
2. Stefano ali ngati Ambuye Yesu pokhala munthu wokhulupirika ndi wopanda cholakwa amene anakonzeka kupereka moyo wake chifukwa cha Uthenga Wabwino.

**Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 6: 5; 8: 4-17, 26-40***
**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 8: 35***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Filipo anali mlaliki amene utumiki wake wa Uthenga Wabwino unkayenda bwino ndipo anali wokonzeka kuchoka ku Samariya ndi kupita ku chipululu ku Gaza kukalalikira Uthenga Wabwino kwa munthu mmodzi amene ankaufuna.
2. Pamene anakhulupirira Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi wake, munthu wa ku Aitiopiya anali wokonzeka kumvera Ambuye pobatizidwa ndipo anali ndi chimwemwe chachikulu mu mtima mwake pamene ankapita kwawo.

## MAWU OYAMBA

Taganizira tanthauzo la kuzunzika chifukwa cha chikhulupiriro chanu ndipo pereka zitsanzo za masiku ano. Fotokozani kuti Akhristu oyambirira pamene ankapita kulalikira Uthenga Wabwino ankakumana ndi zotsutsa kuchokera kwa olamulira dziko ndi atsogoleri achipembedzo a nthawi imeneyo. Ngakhale ankawalemekeza ndi kuwamvera, iwo anali okonzeka kusamvera malamulo onse amene ankatsutsana ndi Malamulo a Mulungu, mpaka kuphedwa.

Filipo anali mmodzi mwa anthu asanu ndi awiri amene anasankhidwa pa ***Machitidwe 6: 5*** kuti aziyang'anira zochitika mu mpingo. Kenaka anakhala mlaliki ndipo anabweretsa Uthenga Wabwino ku Samariya. Ali m'kati mwachitsitsimutso mu Samariya, Ambuye Yesu anamuwuza kuti apite ku Gaza, ku chipululu, kuti akakumane ndi munthu mlendo wosowa thandizo wa ku Aitiopiya ndi cholinga chofuna kugwiritsa ntchito Filipo kuti munthuyo apulumutsidwe ndi kubatizidwa. Filipo atachita zimenezi, nthawi yomweyo anachotsedwa modabwitsa ndipo anakapitiriza kulalikira Uthenga Wabwino ku madera ena.

## KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Khalidwe la Stefano akuti ndi la Mkhristu amene anali wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, komanso khalidwe labwino ndi mbiri yabwino, ***(Machitidwe 6: 3)*** wodzaza ndi chikhulupiriro, mphamvu ***(Machitidwe 6: 8)*** ndi nzeru ***(Machitidwe 6: 10)*** ndipo amene ankatanganidwa pogwira ntchito ya Ambuye ***(Machitidwe 6: 8)***.
2. Atamangidwa ndi atsogoleri a Ayuda popanda chifukwa, anadziteteza powakumbutsa kuti dziko lonse la Ayuda lakhala likukana Ambuye Yesu koma tchimo lawo lalikulu linali kupachika 'Munthu wosalakwa kapena Wolungama'. ***(Machitidwe 7: 52)***
3. Ngakhale anazunguliridwa ndi gulu la anthu lokwiya limene linamugenda miyala ndi kumupha, Stefano monga Ambuye Yesu anapereka mzimu wake kwa Ambuye ***(Machitidwe 7: 59)*** ndi kupempherera amene ankamupha ndi 'kugona tulo' ***(Machitidwe 7: 60)***. Mawu akuti 'kugona' apa akutanthauza kuti thupi lake ndi limene 'likugona' mpaka pamene Ambuye adzabweranso kudzatenga Mpingo wake.

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro 2.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukonzeka kufa!

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Filipo anamvera Lamulo la Mulungu loti apite kukalalikira munthu wa ku Aitiopiya.
2. Munthu wa ku Aitiopiya anachokera ku Afirika ndi kupita ku Yerusalemu, koma anachokako wosamvetsetsa za Uthenga Wabwino. Iye ankawerenga Baibulo kuti amvetsetse. ***(8: 27-28)***
3. Filipo, motsogozedwa ndi Ambuye, anafika pa nthawi yoyenera ndi kumufotokozera zomwe zili pa Yesaya 53. Iye anamuonetsa kuti chaputala chimenechi chinkanena za moyo ndi imfa ya Ambuye Yesu. ***(8: 34-35)***
4. Munthu wa ku Aitiopiya anakhulupirira Ambuye Yesu ndipo nthawi yomweyo anabatizidwa pomizidwa m'madzi ndipo anapita kwawo akusangalala. ***(8: 36-38)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro 2.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Filipo.

## KUKUMBUTSANA

Onetsetsani kuti ophunzira amvetsa Vesi Yoloweza ndipo kambiranani nawo kuti vesiyi ikufotokoza chidule cha phunziro lonse ndipo zikukhudza Ambuye Yesu pamodzi ndi Stefano poonetsa kuti onse anapempherera amene ankawapha ***(Luka 23: 34 ndi Machitidwe 7: 60)*** ndipo onse anapereka mizimu yawo kwa Mulungu ***(Luka 23: 46 ndi Machitidwe 7: 59)***.

Lumikizani phunziroli ndi ***Yesaya 53***. Fotokozani kuti chaputala chimenechi chinalembedwa pakati pa zaka 740-680 BC ndi kuti ulosi wa Yesaya ukunena mwachindunji za imfa, kuyikidwa m'manda, kuukitsidwa ndi kukwezedwa kwa Ambuye Yesu.

## KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Kodi taphunzira chiyani za, m'nthawi yovuta, kukhala wokhulupirika kwa Ambuye Yesu?
2. Kodi pa kudzipereka kwa Stefano kwa Ambuye tikuphunzira chiyani lero, pamene malamulo ena a boma akutsutsana ndi Malemba Oyera?

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Pamene Ambuye atiyitana kuti tigwire ntchito yake, kodi timamvera popanda mafunso monga Filipo anachitira?
2. Kodi ife tikukwaniritsa motani udindo wathu monga Akhristu pofuna kukhala mboni za Ambuye Yesu pofuna kuona ena akubwera kwa Iye?
3. Kodi ophunzira aganizirapo zobatizidwa ngati njira yosonyeza pagulu chikhulupiriro chawo?

| | B5 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 3 – Antchito a Ambuye<br>Mutu – Kukonzeka kumvera! | B5 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 3 – Akhristu Oyambirira<br>Mutu – Korneliyo |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 8:1- 5, 26-40***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 16: 31***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kumvera msanga kwa Filipo ndi kupanda mafunso zinachititsa kuti Ambuye amugwiritse ntchito kubweretsa munthu wa ku Aitiopiya kwa Ambuye.<br>2. Munthu wa ku Etiopiya anapita kwawo akusangalala chifukwa cha kumvera kwake Ambuye. | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 10: 1-8, 23-48***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 10: 43***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Uthenga Wabwino ndi wa aliyense, Myuda ndi wa Mitundu.<br>2. Korneliyo ndi a pa banja ake anali oyamba pakati pa amitundu kukhala okhulupirira Ambuye Yesu. |
| MAWU OYAMBA | Fotokozani kuti nthawi zina Mulungu amafuna kuti tichite chinthu chosiyana kwambiri ndi chomwe timayembekezera kumachita.<br>Fotokozani kuti Filipo ankaona Ambuye akuchita ntchito yayikulu mu Samariya. Koma, Ambuye anamulamula kuti achoke kumene anthu ambiri ankatembenuka mtima ndi kupita ku chipululu cha ku Gaza kuti akathandize moyo wauzimu wa munthu mmodzi, munthu wa ku Aitiopiya. | Fotokozani za ubale wa Ayuda ndi Amitundu, ndi kuti Ayuda sankayanjana kapena kulowa m'nyumba za Amitundu.<br>Korneliyo anali msilikali wa Chiroma (wa Mitundu), amene ankakhala ku Kaisareya ndipo anali waudindo pakati pa asilikali anzake. Ngakhale ankakhala moyo wangwiro, sankadziwa Ambuye Yesu. Komatu iye ankafunitsitsa atakhululukidwa machimo ake ndipo Mulungu anachita pobweretsa Petro amene anadzalalikira Uthenga Wabwino kwa iye ndi a pa banja lake. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Pamene Filipo anakumana ndi munthu wa ku Aitiopiya, munthuyo ankawerenga ***Yesaya 53: 7-8*** ndipo Filipo anapeza mwayi woyankhula kwa iye za moyo ndi imfa ya Ambuye Yesu.<br>2. Munthu wa ku Aitiopiya anaphunzira kuchokera kwa Filipo kuti amene Yesaya analemba za Iye anali Ambuye Yesu amene anafa pa mtanda kuti akhale Mpulumutsi wake. Choncho munthu wa ku Aitiopiya anazindikira kuti anali wochimwa ndipo analandira Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi wake atakhulupirira. ***(Machitidwe 8: 34-38)***<br>3. Filipo anafotokoza za mwayi wobatizidwa kwa munthu wa ku Aitiopiya ndipo pamene anapeza madzi, Filipo anamubatiza. Antchito amene anali ndi munthuyu sanachitire umboni wokha obatizidwa komanso anaona chisangalalo chimene munthuyu anali nacho chifukwa anali wotsatira wa munthu wotchedwa Yesu wa ku Nazarete m'masiku amenewo.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukonzeka kumvera! | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Tsiku lina Korneliyo anaona masomphenya, 3 koloko masana, pamene mngelo wa Mulungu anabwera kwa iye ndi kumuwuza kuti atumize anthu ku Yopa kwa Petro. ***(10: 3-6)***<br>2. Petro atafika ku nyumba ya Korneliyo anapeza kuti kunali anthu enanso amene ankafuna kumva zomwe alalikire. ***(10: 24)***<br>3. Petro anayankhula kwa anthu powauza kuti Mulungu sakondera – chipulumutso chake ndi kwa aliyense, Ayuda ndi Amitundu. ***(Machitidwe 10: 34-35)***<br>4. Petro analalikira kwa amene anasonkhanawo za moyo, imfa ndi kuuka kwa Ambuye Yesu ndipo anatsiriza ndi kuwauza kuti ngati akhulupirira Iye adzakhululukidwa machimo awo. ***(10: 38-44)***<br>5. Izi ndi zimene anthu Amitundu amene anasonkhanawo anachita, ndipo anali oyamba pakati pa anthu Amitundu kukhulupirira Ambuye Yesu ndi kubatizidwa. ***(Machitidwe 10: 47-48)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Korneliyo. |
| KUKUMBUTSANA | Lumikizani phunziroli ndi ***Yesaya 53*** ndi kukambirana makamaka ***vesi 7 ndi 8***. Monga nkhosa imakhalira duu poyimeta, Ambuye Yesu anapirira ululu wa pa mtanda. Iye sanaweruzidwe mwachilungamo ndipo anaphedwa pakati pa moyo wake ndi kupachikidwa chifukwa cha machimo athu. | Ganizirani zoti Petro anali Myuda ndipo akulowa m'nyumba ya wa Amitundu. Onani ***Machitidwe 10: 9-17*** kuti muone zomwe anauzidwa kuti achite, ndi maganizo ake pa kupititsa Uthenga Wabwino kwa Amitundu. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kuti timvetse Akhristu omvera akhoza kukhala dalitso kwa onse - omwe ndi Akhristu komanso si Akhristu.<br>2. Chikhulupiriro cha munthu aliyense mwa Ambuye Yesu chidzitsatana ndi kubatizidwa. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kuti timvetse kukhululukidwa kwa machimo kulipo kwa aliyense, posatengera mtundu wa munthu, chikhalidwe ndi chipembedzo.<br>2. Kambiranani kuti tsopano tili ndi Baibulo loti litiphunzitsa zoyenera kuchita pa miyoyo yathu ndi zoti tichite kuti tikhululukidwe machimo athu. |

| | B5 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 4 – Antchito a Ambuye<br>Mutu – Kukonzeka kupita! | B5 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 4 – Akhristu Oyambirira<br>Mutu – Barnaba |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 10: 1-20, 24-29, 33-43***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 10: 43***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ngakhale Korneliyo anali munthu wabwino kwambiri, pankafunika wina kuti amuwuze momwe angakhalire Mkhristu.<br>2. Petro anaphunzira kudzera m'masomphenya kuti Uthenga Wabwino si wa Ayuda okha komanso ndi wa munthu aliyense. | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 4: 32-37; 9: 26-31; 11: 19-30***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 11: 24***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ife sitingakhale Akhristu chifukwa cha ntchito zabwino zimene tikuchita.<br>2. Akhristu amachita ntchito zabwino chifukwa 'kukoma mtima' ndi chimodzi mwa chipatso cha Mzimu m'moyo wa Mkhristu. ***(Agalatiya 5: 22)*** |
| **MAWU OYAMBA** | Za m'phunziro ili zikuchitika ku Kaisareya, mzinda wa m'mbali mwa nyanja. Korneliyo anali mkulu wa asilikali a Chiroma ndipo ankalamulira asilikali 100. Iyeyu anali wa m'gulu la Italiya. Koma anali munthu amene ankafunafuna Mulungu. Iye anali wa Amitundu, koma nthawi iyi n'kuti Petro atalalikira Uthenga Wabwino kwa Ayuda okha. | Ife tikumva za Barnaba koyamba pa ***Machitidwe 4: 36***. Tanthauzo la dzina lake ndi "mwana wachilimbikitso". Iye ankachokera ku chilumba cha Kupro ndipo Baibulo likutiwuza kuti anagulitsa munda wake ndi kubweretsa ndalamazo kwa Atumwi. Iye anachita zinthu molingana ndi dzina lake chifukwa kupereka kwake kunalimbikitsa kwambiri Atumwi. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mngelo anamuwuza Korneliyo m'masomphenya kuti atume anthu apite ku Yopa, tawuni ya kummwera kwa Kaisareya akayitane Simoni Petro. ***(Machitidwe 10: 3-6)***<br>2. Tsiku lotsatira, Petro anaona masomphenya pamene anali pa denga la nyumba ya Simoni pamene anapita kukapemphera. Mulungu anawuza Petro kuti Uthenga Wabwino sunali wa Ayuda okha komanso unali wa Amitundu. Mulungu amaona magulu awiri a anthu – amene ndi ake ndi amene si ake! ***(Machitidwe 10: 9-16)***<br>3. Petro atafika ku nyumba ya Korneliyo, iye anavomereza kuti ankakhulupirira kuti Mulungu ankakonda dziko la Israyeli lokha basi, Ayuda, koma anaphunzira kuti Mulungu sakondera. ***(Machitidwe 10: 34-35)***<br>4. Petro analalikira Uthenga Wabwino kwa amene anali m'nyumbamo ndipo anatsindika kuti chipulumutso ndi 'aliyense amene akhulupirira Iye'. ***(Machitidwe 10: 43)***<br>5. Anthu amene anali m'nyumbamo anakhulupirira ndi kubatizidwa ndipo ichi chinali chiyambi cha Amitundu kulowa mu Mpingo.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukonzeka kupita! | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Barnaba anali mtumiki wa Ambuye wodzipereka kwambiri ndi wosadzikonda. Iye anagwiritsa ntchito nthawi yake ndi chuma chake kuthandiza anthu ena. Iye ankafuna kuona anthu akubwera ndi kudziwa Ambuye Yesu ndiponso ankafuna kuthandiza amene anali ndi zosowa zofunika pa moyo wa munthu. Chifukwa cha chimenechi iye anatchedwa 'munthu wabwino'. ***(Machitidwe 11: 24)***<br>2. Barnaba anaonetsa moyo wachifundo kwa Paulo. ***(Machitidwe 9: 27)*** Iye anaonetsa chikondi kwa Paulo pamene Akhristu a mu Yerusalemu ankaopa kumulandira.<br>3. Barnaba anatumidwa ndi mpingo mu Yerusalemu kuti akalimbikitse Mpingo watsopano ku Antiokeya ndipo ali kumeneko anthu ambiri anatembenukira kwa Ambuye. Iye analimbikitsa Akhristu atsopano a ku Antiokeya kuti 'akhale woona mwa Ambuye.' ***(Machitidwe 11: 23)*** Mwina panalibenso mawu anzeru amene anayankhulidwa kwa otembenuka mtima atsopano kuposa awa!<br>4. Barnaba atafika ku Antiokeya ndi kuona zonse zimene zinkachitika, iye anazindikira kuti ankafunika wina woti amuthandize, choncho anapita ku Tariso ndi kukatenga Saulo amene adzamuthandize. ***(Machitidwe 11: 25-26)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Barnaba. |
| **KUKUMBUTSANA** | Phunzirani Vesi Yoloweza ndi kambirana momwe ikufotokozera mwachidule phunziro la lero lonse. Ndiponso onetsani ophunzira mawu akuti 'aliyense amene akhulupirira iye' - ***Yohane 3: 15-16.*** | Onaninso phunziroli pofunsa mafunso amene athandiza ophunzira kuyankha mafunso a mu Phunziro 4 molondola. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kugawana Uthenga Wabwino ndi achinyamata a mitundu ina.<br>2. Fotokozani ***Machitidwe 10: 34-35*** m'mawu anu. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kuonetsa 'kukoma mtima' m'miyoyo yathu monga Akhristu.<br>2. Kukhala woona mtima mwa Ambuye Yesu monga Akhristu.<br>3. Kulimbikitsa Akhristu ena amene akudutsa nthawi zovuta. |

| | **B6 – KALASI Lachitatu**<br>**Phunziro 1 – Moyo wa Yosefe**<br>**Mutu – Mnyamata wa maloto** | **B6 – KALASI Lachinayi**<br>**Phunziro 1 – Yakobo ndi banja lake**<br>**Mutu – Ku Harana** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 37: 1-11***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 37: 8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yosefe ali mnyamata wa zaka 17, Mulungu anamuyankhula m'maloto ndi kumuwuza chikonzero chimene anali nacho pa moyo wake.<br>2. Tchimo la nsanje ndi loyipa pamaso pa Mulungu ndipo limabweretsa lina loopsa, choncho tikuyenera kulipewa. | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 29: 1-30***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Agalatiya 6: 7***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yakobo anali atanamiza abambo ake ndi m'bale wake ndipo anali atathawira ku Harana kwa amalume ake.<br>2. Mulungu amalamulira chilichonse ndipo amachita zinthu pa nthawi yake.<br>3. Ngati tidzala zoyipa m'miyoyo yathu, tikuyenera kuyembekeza kudzakolola zoyipa. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ophunzira za makolo a Yosefe, Abrahamu, Isake ndipo tsopano tili pa Yakobo ndi banja lake.<br>Yosefe anali mmodzi mwa ana a Yakobo ndipo amayi ake anali Rakele. Iye anali m'busa wa ziweto. Iye anali ndi mng'ono wake wotchedwa Benjamini ndipo ndi nthawi imene ankabadwa Benjamini pamene amayi ake, Rakele, anamwalira. Yakobo anali ndi akazi anayi, koma iye ankakonda kwambiri Rakele, moterenso ankakondanso kwambiri ana ake awiri aamuna, Yosefe ndi Benjamini. | Kumbutsani ophunzira za makolo a Yakobo. Yakobo anali mwana wa Isake ndi Rebeka ndi m'bale wake Esau. Iye ankakhala ku Beereseba ndipo anathawa ndi kupita ku Harana ku Mesopotamiya chifukwa Esau ankafuna kumupha atamubera udindo wake wa woyamba kubadwa. (Lembani mwachidule nkhaniyi.) Yakobo anali ndi zaka 77 pamene anachoka ku Beereseba; iye anagwira ntchito kwa amalume ake, Labani, zaka makumi awiri, zaka 33 anali atabwerera ku Kanani, ndipo zaka zina zisanu ndi ziwiri zomaliza za moyo wake anali ku Aigupto. Ulendo wochokera ku Beereseba kupita ku Harana unali wa makilomita 805. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Abale ake ankamuda Yosefe chifukwa ankawuza Yakobo zoyipa zimene ankachita ndipo Yakobo ankamukonda chifukwa anali mwana wa Rakele ndipo anabadwa Yakobo atakalamba. ***(37: 2)***<br>2. Mkanjo wa mitundu yambiri unali wautali okhala ngati malaya omwe unkaonetsa kuti Yakobo ankakonda kwambiri Yosefe, zomwe zinabweretsa nsanje ndi udani m'mitima mwa abale ake. ***(37: 3 ndi 4)***<br>3. Maloto woyamba wa Yosefe, mitolo khumi ndi umodzi ya tirigu inkagwadira mtolo wa khumi ndi chiwiri omwe unali ulosi woti tsiku lina abale ake adzamugwadira. Maloto achiwiri unalinso ulosi woti abale ake pamodzi ndi Yakobo (dzuwa) adzamugwadira ndi Leya (mayi ake aakulu) (mwezi) pakuti Rakele n'kuti atamwalira. ***(37: 5-11)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mnyamata wa maloto. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nthawi ya Mulungu inali yabwino pakuti Mulungu anatsogolera Yakobo ku dera kumene abusa aziweto a ku Harana ankadyetsera ziweto zawo komanso kumene Rakele anafika ndi ziweto zake.<br>2. Yakobo anagwira ntchito kwa amalume ake; iye ankafuna kukwatira Rakele koma Labani anamunamiza ndipo anakwatira Leya, mwana wake wamkazi woyamba. Iye anagwiranso ntchito zaka zina zisanu ndi ziwiri kuti akwatire Rakele. Kenaka anagwiranso ntchito zaka zina zisanu ndi ziwiri. ***(Genesis 29: 15-30)***<br>3. Yakobo ananamiza abambo ake ndi m'bale wake ndipo tsopano iye akunamizidwanso ndi amalume ake. Yakobo anadzala chinyengo ndipo tsopano amakolola chinyengonso!<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 1.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Ku Harana. |
| **KUKUMBUTSANA** | Onaninso phunziroli pofunsa mafunso amene athandize ophunzira kuyankha mafunso a Nthawiyabaibulo Phunziro 1. | Gwiritsani ntchito mapu kuti ophunzira akhale ndi chithunzi m'maganizo mwawo cha ulendo wa Yakobo kuchokera ku Beereseba (Kumadzulo wa Mtsinje) mpaka ku Harana (ku Mtsinje wa Firate) m'dziko la Suria lero. Mutha kuwafotokozera za mikangano imene ikuchitika lero ku mayiko a Kummawa lero ku Suria, Yordano ndi Iraki chifukwa anthu kumeneku amafuna kuchita zofuna zawo m'malo mofunafuna chifuniro cha Mulungu pa moyo wawo. Kudzikonda kwa Yakobo kukuonekerabe m'miyoyo mwa anthu lero – izi zili chomwechi chifukwa tinabadwa ochimwa! |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Mulungu ali ndi chikonzero chamoyo wa aliyense. Tikakhulupirira Ambuye Yesu monga Mpulumutsi, Iye adzakwaniritsa chikonzero chake mwa ife. Ife timachita zomwe atimaphunzitsa m'Baibulo ndipo timapemphera tsiku ndi tsiku kuti Iye azititsogolera m'njira zimene zimamukondweretsa.<br>2. Tikuyenera kupewa tchimo la nsanje m'mitima mwathu; Baibulo limati tchimo limeneli ndi 'ndilaliwuma ngati manda'. ***(Nyimbo ya Solomoni 8: 6)*** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Tikuyenera kudziwa kuti ngati sitilapa tchimo lathu ndi kukhulupirira Mpulumutsi pa chipulumutso chathu, tidzakolola zotsatira za uchimo wathu.<br>2. Ngati ndife Akhristu ndiye tachimwa tikuyenera kuvomereza msanga tchimo lathu kwa Ambuye Yesu kuti atikhululukire ***(1 Yohane 1: 9)***, ndi kutembenuka kusiya tchimo lisanabweretsa zoyipa zomwe zidzasautsa miyoyo yathu. |

| | **B6 – KALASI Lachitatu**<br>**Phunziro 2 – Moyo wa Yosefe**<br>**Mutu – Chidani cha abale ake** | **B6 – KALASI Lachinayi**<br>**Phunziro 2 – Yakobo ndi banja lake**<br>**Mutu – Ku Penieli** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 37: 12-36***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aroma 6: 12***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Tchimo limayamba pang'ono m'miyoyo yathu ndipo ngati sitipempha Ambuye Yesu kuti atikhululukire lidzakula ndi kulamulira miyoyo yathu.<br>2. Tikatsutsika mu mtima chifukwa cha tchimo lathu, ndi zofunika kwambiri kuti tivomereza nthawi yomweyo pamaso pa Ambuye Yesu. | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 32: 1-32***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 32: 11***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yakobo anapemphera kwa Mulungu chifukwa anathedwa nzeru ndipo ankafuna chitetezo cha Mulungu.<br>2. Pomaliza Yakobo akupereka moyo wake kwa Mulungu ndipo atavomera pamaso pa Mulungu kuti dzina lake ndi Yakobo, kutanthauza 'chinyengo'. Mulungu anasintha dzina lake ndi kukhala Israyeli, kutanthauza 'kalonga wa Mulungu.' |
| **MAWU OYAMBA** | Bwerezani nkhani ya Yosefe ndi kukumbutsa ophunzira za kusagwirizana komwe kunali m'banja la Yakobo ndi zifukwa zake. Pa ***Genesis 27***, Yakobo anapusitsa abambo ake polandira madalitso m'malo mwa Esau. M'phunziro lino tikuona ana a Yakobo akumunamiza pomuonetsa chikopa cha mbuzi cha magazi. N'koyenera kuganiza kuti mwina Yakobo anakumbukira pamene ana ake anamunamiza motere. Ululu wachinyengo ukumvekanso m'moyo wa Yakobo nthawi imeneyi! | Kambiranani za misonkhano imene ophunzira anachitapo ndi anthu olemekezeka. Fotokozani kuti m'phunziro lino tikulingalira za kukumana ndi Mulungu ndi zotsatira zake pa moyo wa Yakobo. Munthu amene analimbana ndi Yakobo ***(vesi 24)*** sanalinso wina koma Ambuye mwini. Werengani ***Hoseya 12: 4***. Komanso onani pamene Ambuye (i) akuonekera kwa Mose m'chitsamba choyaka moto ***(Eksodo 3: 1-22)***; (ii) akuonekera kwa Mose nthawi ziwiri pamene ndondo yake inasanduka njoka ndi dzanja lake kukhala la khate ***(Eksodo 4: 1-17)***; (iii) akuonekera kwa Yesaya ndi funso ndipo Yesaya akuyankha ***(Yesaya 6)***; (iv) akuonekera kwa Saulo pa njira yopita ku Damasiko (Machitidwe 9: 1-19). Tsindikani kuti anthu onsewa anali ndi mkumano wapamwamba kwambiri ndi Ambuye komanso osawayiwalika kwa iwo. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Udani wa abale ake pa Yosefe unafika poti anamuponya m'dzenje. ***(37: 12-18)***<br>2. Abale a Yosefe anamugulitsa kwa Aismayeli ndalama zasiliva makumi awiri, (otchedwanso Amidyani) amene ankapita ku Aigupto. ***(37: 25-28)***<br>3. Abambo a Yosefe, Yakobo, anamva chisoni kwambiri pamene abale ake ankawafotokozera zonama. Iwo anaonetsa chovala chomwe anachiviika m'magazi a mbuzi ndipo Yakobo anaganiza kuti mwana wake wafa. ***(37: 31-35)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 2.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Chidani cha abale ake. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yakobo anali pa ulendo wobwerera ku Kanani kuchokera ku Harana ndipo ankaopa kuti adzaphedwa ndi Esau chifukwa cha zomwe anachita zaka makumi awiri m'mbuyomo. ***(Genesis 27: 41)***<br>2. Yakobo anatumiza magulu atatu motsatana a ziweto, zonse pamodzi 580, kuti zitonthoze Esau. ***(32: 13-21)***<br>3. Yakobo anakhala usiku wonse pa Penieli (nkhope ya Mulungu) – chinthu chosayiwalika pa moyo wake. Mulungu anagulula polumikira tchafu yake ndi kusintha dzina lake la Yakobo ndi kukhala Israyeli. ***(32: 22- 32)***<br>4. Yakobo anamva kuti Esau akubwera ndi amuna 400, choncho anayika banja lake m'magawo awiri ndi cholinga chakuti ngati gawo loyamba laonongedwa, gawo lachiwiri lithawe. ***(33: 1-2)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 2.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Ku Penieli. |
| **KUKUMBUTSANA** | Kambiranani kuti Mulungu ankalamulira zochitika zonse: Aismayeli, ngakhale kuti sankadziwa, ankapereka mayendedwe aulere kwa Yosefe opita ku Aigupto kuti akamugulitse kwa Potifara, mmodzi wa akulu asilikali a Farao. Ndi ku Aigupto kumene Mulungu anakonza kudalitsa kwambiri Yosefe ndi kuti adzakhala wachiwiri wolamulira dziko lonse la Aigupto.<br>Fotokozani ***Salimo 76: 10*** kuti ikuonetsa kuti Mulungu angathe kusintha ukali wa munthu kukhala matamando kwa Iye ndi kuti Iye amaletsa chomwe sichimukondweretsa. | Onaninso Phunziroli ndi kufunsa mafunso ophunzira amene adzawathandiza kuyankha mafunso omwe ali mu Phunziro 2.<br>Aonetseni matanthauzo a mawu awa:<br>Mahanaimu ***(vesi 2)*** – magulu awiri.<br>Yakobo ***(vesi 27)*** – wachinyengo.<br>Israyeli ***(vesi 28)*** – amene amalimbana ndi Mulungu, kapena kalonga wa Mulungu.<br>Penieli ***(vesi 30)*** – nkhope ya Mulungu. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kambiranani ngati ophunzira anakhalapo ndi mkwiyo kapena kukhala ndi nsanje m'mitima mwawo? Ngati ndi choncho, onse akuyenera kuvomereza tchimo lawo kwa Ambuye Yesu ndi kumupempha kuti awapatse mphamvu yokhala moyo opanda zoyipa. Onani ***1 Yohane 1: 7***.<br>2. Phunzirani Vesi Yoloweza ***Aroma 6: 12***, ndi kulimbikitsa ophunzira kuti iyi ikhale fundo yolamulira miyoyo yawo. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Yakobo anatsala yekha ndi Mulungu. ***(vesi 24)*** Monga ochimwa tikuyenera kukumana tokha ndi Mulungu kuti tilandire chipulumutso. Aliyense akuyenera kukumana ndi Mulungu kuti machimo ake akhululukidwe!<br>2. Mngelo analimbana ndi Yakobo ***(vesi 24)*** ndi kumulanda kunyada kwake ndiponso chiphamaso chake. Ndi Mulungu yekha amene angachite zimenezi pa ife.<br>3. Dzina la Yakobo linasintha. Tonse tikuyenera kuti mayina athu asinthenso kukhala Mkhristu? Wokhulupirira? Pamenepo maganizo athu adzasintha, malo athu pamaso pa Mulungu adzasintha, ubale wathu ndi Mulungu udzasintha, ndiponso khalidwe lathu lidzasintha pamaso pa Mulungu. |

| | B6 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 3 – Moyo wa Yosefe<br>Mutu – Wam'ndende wokhulupirika | B6 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 3 – Yakobo ndi banja lake<br>Mutu – Ku Beteli |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 39: 1-6, 19-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 39: 21***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ngakhale Yosefe anali ku Aigupto kutali ndi kwawo, Iye anali wokhulupirika pamaso pa Mulungu ngakhale ankadutsa nyengo zowawa kwambiri.<br>2. Mulungu ankayang'anira Yosefe ndipo anali ndi tsogolo labwino la Yosefe. ***(Aroma 8: 28)*** | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 35: 1-15***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Salimo 37: 7***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pamene Yakobo ankakonzekera kukumana ndi Esau, iye ankafuna thandizo la Mulungu nthawi zonse.<br>2. Monga Akhristu titha kuchoka pamaso pa Mulungu ndi kumayenda m'njira zathu, koma Mulungu satisiya kapena kutitaya.<br>3. Monga Akhristu, timafuna thandizo la Mulungu kuti tithane ndi zofooka zathu za kale ndi mavuto ndi amayesero amene tidzakumana nazo m'tsogolo. |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani kusowa kwa chilungamo komwe kumachititsa anthu osalakwa kumangidwa. Fotokozani momwe zinachitikira ndi Yosefe.<br>Fotokozani kuti m'mayiko ena lero, okhulupirira ali m'ndende. Iwo sali m'ndende chifukwa analakwa koma chifukwa ndi okonzeka kukhala okhulupirika kwa Mulungu, pokhulupirira ndi kumvera zomwe anaphunzira m'Baibulo, momwe angakhalire moyo wawo monga Akhristu. | Yambani phunziroli ndi kufotokoza kuti amene amakhulupirira Ambuye amakhala ndi chitsimikizo kuti Iye amawateteza – muli chitetezo mwa Ambuye.<br>***Salimo 91*** ndi ***Aroma 8***, akuonetsa za chitetezo chimenechi. Mavesi otsatirawa ndi oyenera kuwawerenga monga mawu oyamba komanso zoyenera kudziwa: ***Salimo 91: 2, 15*** ndi ***Aroma 8: 31***. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yosefe anagulitsidwa ndi Aismayeli monga kapolo kwa Potifara, nduna ya nyumba ya ufumu ya Farao. ***(39: 1)***<br>2. Mkazi wa Potifara anayankhula zabodza za Yosefe, anamunenera zabodza ndipo anakaponyedwa m'ndende. ***(39: 7-20)***<br>3. Yosefe anali ndi khalidwe labwino m'ndende ndipo mkulu wa ndende anamusankha kukhala woyang'anira m'ndendemo. ***(39: 21-23)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Wam'ndende wokhulupirika. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mulungu akulamula Yakobo kuti akwaniritse lonjezo limene anachita zaka makumi atatu zapitazo pa ***Genesis 28: 20-22***, ndi kubwerera ku Beteli.<br>2. Yakobo akulamula banja lake kuti achotse milungu yachilendo ndi kuchapa zovala zawo ndipo atachita izi anakhala anthu oopsa kwa anthu osakhulupirirawo. ***(Genesis 35: 2-5)***<br>3. Iye akumanga guwa lansembe ku 'El Beteli', ndipo akupembedza Mulungu amene anamuteteza kwa Esau. ***(Genesis 35: 6-7)***<br>4. Mulungu akukumananso ndi Yakobo ku Beteli ndipo akubwerezanso pangano lake ndi Abrahamu ndi Isake. ***(Genesis 35: 11-13)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 3.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Ku Beteli. |
| **KUKUMBUTSANA** | Onaninso phunziroli pofunsa ophunzira kuti afotokoze momwe Mulungu analepheretsera cholinga cha Satana pa moyo wa Yosefe ndi zomwe Yosefe anachita kuti akhale wokhulupirira wopanda cholakwa, wodalirika ndi wodziwa zochita. | Rakele anabereka mwana amene anamutcha Benoni kutanthauza 'mwana wamasautso' koma Yakobo anamutcha Benjamini, kutanthauza 'mwana wadzanja langa lamanja'. Kambiranani momwe phunziro ili likuonetsera kubadwa kwa wina, Ambuye Yesu Khristu, amene adzapirira masautso a pa mtanda, kenaka ndi kukwezedwa ndi Mulungu kukhala kudzanja lake lamanja Kumwamba. Monga ku Beteli kunali malo achikumbutso kwa Yakobo chonchonso pa Kalvari pali chikumbutso cha Ambuye Yesu Khristu ndi amene amamukhulupirira Iye. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1.Ganizirani zomwe taphunzira za momwe Ambuye Yesu Khristu angatisamalire, ngakhale nthawi zovuta kwambiri ngati tikumudalira ndi kumumvera?<br>2. Monga Mkhristu, sikuti sitingakumane ndi mayesero kapena masautso. Kodi tichite chiyani zimenezi zikabwera pa moyo wathu?<br>3. Pezani anthu ena m'Baibulo amene anamangidwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ife tikuyenera kufuna madalitso a Mulungu pa miyoyo yathu powerenga Baibulo ndi kupempha chitsogozo cha Mulungu tsiku ndi tsiku.<br>2. Funsani ophunzira kuti akambirane chimene chakhala ngati 'Beteli' wawo wofunika kwambiri m'miyoyo yawo.<br>3. Monga Mkhristu, pamene tili pa mavuto, tikuyenera kugwiritsa mawu amene ali pa ***Ahebri 13: 5*** – "Sindidzakusiya konse, kungakhale kukutaya, sindidzakutaya ndithu." |

| | B6 – KALASI Lachitatu<br>Phunziro 4 – Moyo wa Yosefe<br>Mutu – Mtsogoleri watsopano | B6 – KALASI Lachinayi<br>Phunziro 4 – Yakobo ndi banja lake<br>Mutu – Ku Kanani |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 41: 14-49***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 41: 32***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yosefe anapereka udindo kwa Mulungu womasulira maloto awiri ndipo chifukwa cha kudzichepetsa kwake Mulungu anamupatsa udindo waukulu kwambiri.<br>2. Yosefe anali wokhulupirika kwa Mulungu, osati pamene anali m'ndende kokha komanso pamene anali m'nyumba yaufumu, ndipo Mulungu anamusamalira. | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 37: 1-36***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aefeso 4: 31-32***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kukondera kumabweretsa nsanje ndipo nsanje imabweretsa tchimo loopsa ndi zotsatira zake m'miyoyo ya anthu – m'moyo wa anthu ansanje ndi mwa amene akuchitiridwa nsanjeyo.<br>2. Ngakhale abale ake anakhala akutsutsika ndi tchimo limeneli kwa zaka zambiri, kumapeto kwake Yosefe anaulula tchimo lawo kwa abambo ake pamene ankamwalira ndipo anawakhululukira ndi kuyanjana nawo. ***(Genesis 50: 20)*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbukirani nkhani mpaka pamene yafika, ndipo fotokozani kuti Mulungu ankakwaniritsa zolinga zake pa moyo wa Yosefe. Fotokozani kuti chifukwa cha mbiri yabwino ya Yosefe, ***(vesi 39)*** anakwezedwa kukhala wachiwiri wolamulira dziko.<br>Pa ***vesi 42*** mphete ikusonyeza kuti wachoka pokhala kapolo ndipo wasanduka mwana wa mfumu: kupatsidwa zovala zabafuta m'malo mwa zovala za sanza, kupatsidwa mkanda wagolide kusonyeza ulamuliro ndipo anapatsidwa galeta pa ***vesi 43*** kusonyeza kuti tsopano si kapolonso koma ndi mfulu mu ufumu wa Farao.<br>Iye wachoka ku malo achitonzo m'dzenje, pamene anali ndi zaka 17, pa malo aulemerero pamene anali ndi zaka makumi atatu. Iye anali wachinyamata pa udindo wofunika kwambiri! | Fotokozani banja la Yakobo ndi kumene ali tsopano. Yambani phunziro lino poonanso ndime zina za m'Baibulo:<br>(i) ***Salimo 56*** – Kambiranani kuti kwa Akhristu, Mulungu akuwasamalira posatengera zomwe mdierekezi akuwachitira kudzera mwa anthu ena.<br>(ii) ***Mateyu 5: 43-48, Aefeso 4: 22-32*** – Limbikitsani ophunzira kuti akhale ndi moyo ngati wa Khristu kuchokera pa ndime zonsezi pa nthawi ya masautso kapena kutsutsa kuchokera kwa amene sakonda Ambuye kapena otsatira ake, ngakhale zitha kukhala zovuta kwambiri. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Farao anali ndi maloto ndipo anamutenga Yosefe ku ndende kuti adzamasulire maloto. ***(41: 14-16)***<br>2. Yosefe anamasulira maloto awiri a Farao – zaka zisanu ndi ziwiri za zakudya zambiri ndi zaka zisanu ndi ziwiri za njala. Farao anasankha Yosefe kukhala wachiwiri wake ndi woyang'anira ntchito yosunga chakudya. ***(41: 17-40)***<br>3. Kunali tirigu wambiri m'zaka za zakudya zabwino zija, motero kunali kovuta kuwerengera pamene ankasunga. Zaka za njala zisanu ndi ziwiri zija zitafika, panali tirigu wochuluka kwa anthu onse osowa mu Aigupto komanso ndi ku mayiko ena. ***(41: 46-49, 53-55)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mtsogoleri watsopano. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yosefe anali ndi maloto ndipo ananyozedwa ndi abale ake. ***(37: 5-11)***<br>2. Yosefe anapatsidwa mkanjo kapena mwinjiro wa mitundu yambiri ngati chizindikiro cha chikondi cha Yakobo pa iye, koma izi zinakwiyitsa kwambiri abale ake. ***(37: 3-4)***<br>3. Maloto a Yosefe anatanthauza kuti abale ake khumi ndi mmodzi ndi Leya ndi Yakobo (Rakele n'kuti atamwalira) adzamugwadira m'tsogolo.<br>4. Abale a Yosefe anakwiya ndipo anagwirizana zomupha ndipo anamugulitsa kwa Aismayeli (Amidyani). Mosazindikira anakwaniritsa cholinga cha Mulungu pa tsogolo la Yosefe. ***(37: 19-28)***<br>5. Abale monama anapita ndi mkanjo wa Yosefe kwa Yakobo ataunyika m'magazi, amene anaganiza kuti Yosefe anaphedwa ndipo anamulira mwana wake amene ankamukonda. Yakobo 'wachinyengo' tsopano 'wanamizidwa'. ***(37: 31-35)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro 4.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Ku Kanani. |
| **KUKUMBUTSANA** | Funsani ophunzira kuti aganize kuti iwo ndi Yosefe ndipo akulembera abambo ake kalata, yowafotokozera kuti apeza ntchito yatsopano! Kodi alembe chiyani m'kalatamo? | Onaninso Phunziroli pofunsa mafunso kuti:<br>(i) Mutsimikize ngati ophunzira amvetsa kuti Mulungu ndiye akulamulira zochitika zonse pa miyoyo yawo ndi kuti Iye sakufuna kuti abweze 'choyipa ku choyipa'.<br>(ii) Onetsetsani kuti athandizidwa kuti ayankhe mafunso a mu Phunziro 4. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi nkhani imeneyi ikutilimbikitsa motani?<br>2. Kodi mwaphunzira chiyani za kukhala womvera ndi wokhulupirika kwa Mulungu m'moyo wa tsiku ndi tsiku?<br>3. Kodi inu mungayembekezere madalitso otani? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kambiranani ngati ***Aefeso 4: 32*** ndi amene akutsogolera moyo wawo?<br>2. Popeza Ambuye Yesu saonetsa kukondera kwa abwino kapena oyipa, monga Akhristu tikuyenera kukhala ndi munthu aliyense moyenera ndi mwabwino? ***(Mateyu 5: 44-45)*** |

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

**Maphunziro a Kalasi Lachitatu**
- Ophunzira sangatsirize maphunziro awa popanda kuwerenga Baibulo ndipo akuyenera kuwerenga ndime imodzi kapena zambiri.
- Kafunsidwe n'kosiyanasiyana, pena pali mabokosi, pena pali mawu amene akusowa ndi njira zina zambiri.
- Mafunso akonzedwa kuti aziyankhidwa kuchokera m'baibulo la Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero ndi Buku Lopatulika ndi Mawu a Mulungu.
- Cholinga chathu n'chakuti ophunzira onse, kaya akugwiritsa Baibulo la mtundu wanji, azitha kuyankha mafunso.
- Sabata lililonse lili ndi marikisi 20 ndipo pa mwezi pali marikisi 80, ngati munthu wakhonza bwino maphunziro onse.
- Kalasi Lachitatu - Pali marikisi imodzi pa yankho, monga momwe tasonyezera.

**Maphunziro a Kalasi Lachinayi**
- Awa ndi maphunziro ovutirapo kusiyana ndi Maphunziro a Kalasi Lachitatu.
- Muli mafunso ovutirapo ofuna mayankho.
- Marikisi 20 pa sabata ndi marikisi makumi 80 pa mwezi ngati amaliza maphunziro molondola ndiponso mafunso onse ali ndi mayankho ake.

**FUNDO ZA KACHONGEDWE**
Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:
- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembera, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.
Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

**KALASI Lachitatu**
**Ndemanga zina**
"Ntchito yabwino kwambiri! Inu munamvetsa bwino mafunso onse. Ine ndasangalala ndi yankho la funso lotsiriza limene mwaliyankha bwino kwambiri."
"Moni, Yonatani. Ndikuyamika chifukwa cha kulimbikira kwako. Ndi zosangalatsa kwambiri kuti wayesetsa kuyankha mafunso onse. Ine ndalemba mayankho a mafunso ena amene sunayankhe."

**Ndemanga zauzimu**
"Mose anali ndi mavuto ndi ana a Israyeli, koma Mulungu sanamusiye yekha kuti athetse mavutowo."
"Yosefe sanayiwale kuti abambo ake anamuphunzitsa kukonda Mulungu. Iye anakumbukira zimenezi ngakhale anali kutali ndi kwawo."
"Bartimeyu anatsimikiza mtima zofuna kulandira kuchokera kwa Ambuye Yesu. Iye sanakhumudwitsidwe chifukwa tsopano ankatha kuona ndipo anadziwa kuti Ambuye Yesu anali munthu wapadera kwambiri."

**KALASI Lachinayi**
**Ndemanga zina**
"Maphunziro enanso abwino kwambiri. Zikuoneka kuti tsopano ukumvetsa bwino Nkhani za m'Baibulo ndipo ndikukhulupirira kuti wasangalala nazo. Zikomo kwambiri chifukwa chokhala ndi nthawi yokwanira yochita mosamala maphunzirowa. Zikanatheka kuchita mofulumira, choncho ine ndi kuyamika kwambiri."
"Rakele, wayetsetsa ndithu. Ine ndikaona mayankho akowa, zikuonetsa kuti sunamvetse bwino Nkhani za m'Baibulo. Bwanji uwerengenso zimenezi."

**Ndemanga zauzimu**
"Mafanizo nthawi zina amatchedwa nkhani wamba koma zokhala ndi matanthauzo akumwamba kapena ozama. Kodi ungaganizire tanthauzo lozama la fanizo lomwe lili mu Phunziro 3?"
"Stefano anafa imfa yowawa kwambiri, koma iye sanachite mantha ndi imfa, chifukwa ankadziwa kuti anali ndi Mulungu, ndipo ankadziwa kuti akakhala ndi Ambuye Yesu Kumwamba."

## Zoonjezera A – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B1 | Mafanizo | **Kodi mnansi wanga ndi ndani?** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-064-good-samaritan/ |
| | | **Mlimi wachuma** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rich-fool/ |
| | | **Wofesa mbewu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/parable-sower-seed/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-049-parable-sower/ |
| | | **Kukhululukira ena** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/unforgiving-servant/ |
| | | |
| B2 | Zodabwitsa | **Madzi asanduka vinyo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/wedding-cana/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-016-wedding-cana/ |
| | | **Kuchiritsidwe kwa mwana** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-020-officials-son/ |
| | | **Kutsekula maso osaona** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-076-blind-beggar/ |
| | | **Kuchiritsidwa kwa anthu khumi akhate** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-072-ten-leprosy/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ten-leprosy/ |

## Zoonjezera A – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B1 | Mafanizo | **Anthu angongole awiri** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-010-simeon-anna/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-010-simeon-anna/ |
| | | **Kodi mnansi wanga ndi ndani?** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-twelve/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-011-jesus-found/ |
| | | **Munthu wopusa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/john-baptist-jesus/ |
| | | **Phwando lalikulu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-014-jesus-temptation/ |
| | | |
| B2 | Zodabwitsa | **Madzi asanduka vinyo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-016-wedding-cana/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-wedding/ |
| | | **Mwana achiritsidwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-020-officials-son/ |
| | | **Bartimeyu wosaona** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-blind-man/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-blindman-jericho/ |
| | | **Amuna khumi akhate** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-072-ten-leprosy/ |

## Zoonjezera B – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B3 | Betaniya | **Alongo awiri** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-mary-martha/ |
| | | **Chisoni chisanduka chimwemwe!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-070-lazarus-dies/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-071-lazarus-resurrection/ |
| | | **Ulendo wina** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-084-jesus-anointed/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/mary-anoints-jesus/ |
| | | **Ulendo wa ku Yerusalemu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-jerusalem/ |
| | | |
| B4 | Ambuye Yesu | **'Kufa'** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-093-mocking-jesus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-096-jesus-crucifixion/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-098-jesus-dies/ |
| | | **'Kuuka'** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-101-jesus-resurrection/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-102-appearance-mary/ |
| | | **'Kupita'** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-104-appearance-thomas/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-107-jesus-ascension/ |
| | | **'Kubwerera'** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ascension/ |

## Zoonjezera B – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B3 | Betaniya | **M'nyumba** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-mary-martha/ |
| | | **Pa manda** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-lazarus/ |
| | | **Pa chakudya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-anointed/ |
| | | **Ulendo wa ku Yerusalemu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/triumphant-entry/ |
| | | |
| B4 | Ambuye Yesu | **Imfa Yake** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-crucified/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-dies/ |
| | | **Kuuka kwake kwa akufa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-alive/ |
| | | **Kupita Kumwamba** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-ascension/ |
| | | **Kubwera kwake kwachiwiri** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-ascension/ |

| Zoonjezera C – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
| B5 | Antchito a Ambuye | **Kukonzedwa ndi Mulungu!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ascension/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/pentecost/ |
| | | **Kukonzeka kufa!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/stephen-martyred/ |
| | | **Kukonzeka kumvera!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/philip-ethiopian/ |
| | | **Kukonzeka kupita!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/ |
| | | |
| B6 | Moyo wa Yosefe | **Mnyamata wa maloto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-dreams/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joseph-dreams/ |
| | | **Chidani cha abale ake** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-pit/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/joseph-slave/ |
| | | **Wam'ndende wokhulupirika** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joseph-prison/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-prison/ |
| | | **Mtsogoleri watsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-pharaoh-dreams/ |

| Zoonjezera C – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
| A5 | Akhristu Oyambirira | **Stefano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/stephen-martyred/ |
| | | **Filipo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/philip-simon/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/philip-ethiopian/ |
| | | **Korneliyo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/ |
| | | **Barnaba** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-conversion/ |
| | | |
| B6 | Yakobo ndi banja lake | **Ku Harana** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-wedding/ |
| | | **Ku Penieli** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-esau-reunited/ |
| | | **Ku Beteli** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-esau-reunited/ |
| | | **Mu Kanani** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/josephs-dreams/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-pit/ |

© Bible Educational Services 2020

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 03/2024
(Chichewa)